Kuyamba Moyo Watsopano mwa Yesu
Nkhani Zoona Zochokera mu Buku la Mateyu
Kubwera Koyamba ndi Kwachiwiri Kwa Yesu
Phunziro 1, Mateyu 1 ndi 24

By Christy Akins Brawner

"Chifukwa chake dikirani, pakuti simudziwa tsiku lake lakufika Ambuye wanu…khalani inunso okonzekeratu; chifukwa munthawi m'mene simuganizira, Mwana wa munthu adzadza." Mateyu 24:42,44

*Ngati nkungatheke, munthu aliyense mu gulu ili amene amadziwa kulemba ayenera kubweretsa kope ndi cholembera kapena pensulo ku maphunzirowa.

Mu nthawi imene Aroma analamulira ku dziko lodziwika kunali namwali wamng'ono m'dziko la Israeli dzina lake Maria amene anapalidwa ubwenzi ndi mnyamata dzina lake Yosefe. Tsopano Maria anali ndi pakati asanakhale limodzi ndi Yosefe. Nthawi imene Yosefe atazindikira anafuna kuthetsa ubwenzi wawo. Tsono, usiku wina anatsimikiza mtima wake kuchita izi, kuopa kumchititsa manyazi Maria.

Pamene Yosefe anaganizira zimenezi, mngelo wa Ambuye anaonekera ndi Yosefe namuuza iye kuti apitirize kukwatira Maria chifukwa iyeyo sanamnamize, koma pakati pamene ali napopa ndi pa Mzimu Woyera. Mngelo anamuuza kuti adzabereka mwana amene analonjezedwa ndi aneneri a Chiyuda akale. Mwana amene adzabadweyo ndi amene mneneri Yesaya analosera m'mene iye ananena, "Namwali adzakhala ndi Mwana nadzabala mwanayo ndipo adzamutcha dzina lake Imanuele, lomasulidwa "Mulungu ali nafe."

Yosefe anakhulupirira mngelo, natenga Maria kukhala mkazi wake. Komabe ngakhale zinali chomwecho sanagone limodzi. Anayembekezera kufikira kubadwa kwake kwa Yesu, kunena kuti anabadwa ndi namwali wosadziwa mwamuna. Yosefe anamtchula mwanayo dzina lake Yesu.

Mawu a Mulungu amafotokozera maulosi ambiri a kubwera kwake kwa Yesu. Kubadwa kwake kunalosedwa m'Chipangano Chakale, pamodzi ndi zochitika zotsogolera kufika ku imfa ndi kuuka kwa akufa kwake. Yesu mwini wake ananena kuti anali ndani ndi zimene Iye adzachita. Maulosi ena a Yesu ndiponso maulosi ena ochokera m'Chipangano Chakale sanakwaniritsidwe mpaka tsopano. Maulosi amenewa amatiuza kuti Yesu adzabweranso kwachiwiri pa dziko. Kubwera kwake koyamba kunali modzichepetsa chifukwa Iye anabwera monga mtumiki wozunzidwa. Koma Buku Lopatulika liphunzitsa kuti kubwera kwake kwachiwiri kudzakhala kosiyana ndithu ndi koyamba.

Yesu analankhula ndi ophunzira ake za kubwera kwake kwachiwiri pamene anawaphunzitsa iwo ku phiri la Azitona. Anawafotokozera zimenezi poyankha funso lawo lakuti, "Chizindikiro cha kufika kwanu ndi chiyani, ndi cha mathedwe a nthawi ya pansi pano?"

Yesu anawayankha iwo mochenjeza nati, "Yang'anirani asasokeretse inu munthu. Pakuti ambiri adzafika m'dzina langa, nadzanena, 'Ine ndine Khristu,' nadzasokeretsa anthu ambiri. Koma inu mudzayamba kumva za nkhondo, ndi mbiri za nkhondo; onani, musadere nkhawa; pakuti kuyenera kuti izi zioneke; koma chitsirizo sichinafike. Pakuti mtundu umodzi wa anthu udzukirana ndi mtundu wina, ndi ufumu ndi ufumu wina; ndipo kudzakhala njala ndi zivomezi m'malo akuti akuti. Koma ndizo zonsezi zowawa zoyamba.

"Pamenepo adzakuperekeni ku nsautso, nadzakuphani; ndipo anthu a mitundu yonse adzadana nanu chifukwa cha dzina langa. Ndipo pomwepo ambiri adzakhumudwa, nadzaperekana wina ndi mnzake. Ndipo aneneri onama ambiri adzauka nadzasokeretsa anthu ambiri. Ndipo chifukwa cha kuchuluka kwa kusayeruzika, chikondano cha anthu aunyinji chidzazirala. Koma iye wolimbika chilimbikire kufikira ku chimarizo, yemweyo adzapulumuka. Ndipo Uthenga uwu Wabwino wa Ufumu wa Kumwamba udzalalikidwa pa dziko lonse lapansi, ukhale mboni kwa anthu a mitundu yonse; ndipo pomwepo chidzafika chimarizo.

"Padzakhala masauko akulu monga sipadakhale otero kuyambira chiyambi cha dziko kufikira tsopano ndipo sipadzakhalanso. Ndipo akadaleka kufupikitsidwa masiko awo, sakadapulumuka munthu aliyense: koma chifukwa cha osankhidwawo masiku awo adzafupikitsidwa.

“Tsono musakhulupirire aneneri onama ndi akhristu onama amene adzayenda malo ndi malo nadzaonetsera zizindikiro ndi zodabwitsa. Anthu amenewa akungofuna kusokeretsa anthu, ngakhale, ngati nkotheka, iwonso amene analandira Yesu m’miyoyo yawo.

“Koma tsono, tsiku lina, monga mphezi imang’animira ndi kuwala kuchokera kum’mawa nionekera kumadzulo, kotero kudzakhalanso kufika kwake kwa Mwana wa munthu. Atapita mavuto a masiku awo, dzuwa lidzadetsedwa, ndi mwezi sudzaonetsa kuwala kwake, ndi nyenyezi zidzagwa kuchokera kumwamba, ndi mphamvu za kumwamba zidzagwedezeka. POMWEPO padzaoneka m’thambo chizindikiro cha Mwana wa munthu; ndipo anthu a mitundu yonse ya pa dziko lapansi adzalira, ndipo adzapenya Mwana wa munthu akudza pa mitambo ya kumwamba ndi mphamvu ndi ulemerero waukulu. Ndipo Iye adzatumiza angelo ake ndi kudzamveka lipenga lamphamvu, ndipo adzasonkhanitsa kuchokera ku mphepo zinayi anthu onse amene anapereka miyoyo yawo kwa Yesu Khristu, kuyambira malekezero a dziko lapansi kufikira malekezero ake ena.

“Koma za tsiku lake kapena nthawi yake, sadziwa munthu aliyense, angakhale angelo a kumwamba, kapena Mwana, koma Atate yekha.

“Choncho khalani inunso okonzekeratu; chifukwa mu nthawi m’mene simuganizira, Mwana wa munthu adzabwera.”

MAFUNSO

1. Kodi Yesu anabadwira m’dziko liti?
2. Kodi maina a makolo ake a Yesu pa dziko lino lapansi anali ayani?
3. Zozizwitsa zinali ziti za kubwera kwake kwa Yesu pa dziko lapansi?
4. Mneneri Yesaya analosera kuti Yesu adzabadwira kwa namwali, ndipo adzamutcha dzina lake “Imanuele.” Kodi tanthauzo la dzina ili ndi chiyani?
5. Pamene Yesu anakhala ndi ophunzira ake ku phiri la Azitona, kodi anamfunsa Iye chiyani?
6. Yesu anawauza kuti ayenera kusamala kuti asasokeretsedwa ndi anthu otani?
7. Iye ananena kuti anthu ambiri adzabwera nazitcha ndani?
8. Yesu anafotokozera zinthu zinayi zoopsya zimene zidzachitika padziko lonse lapansi. Kodi zinthu izi zinayi zinali chiyani?
9. Yesu ananena kuti omtsatira Iye adzavutidwa chifukwa amakhulupirira Khristu. Kodi ndi zinthu ziti zina zimene Yesu ananena kuti anthu adzachitirana wina ndi mnzake?
10. Yesu ananena kuti aneneri onama adzakhala ndi mphamvu zochita zinthu zina zimene ngakhale omtsatira Iye adzatha kupusitsidwa. Zina za izi zinali ziti?
11. Yesu ananena kuti kubwera kwake kudzakhala ngati chiyani chomwe chofanizira chimodzi cha zolengedwa?
12. Kodi Yesu akabweranso, chidzachitika chiyani ndi dzuwa, mwezi ndi nyenyezi?
13. Angelo adzayimbira chipangizo chotani posonkhanitsa otsatira onse a Yesu?
14. Kodi anthu ake a Mulungu adzasonkhana kuti?
15. Ndi yani yekha amene akudziwa tsiku limene Yesu adzabweranso?
16. Kodi ndiyenera kuchita chiyani ngati wina achita zozizwitsa zina popanda dzina la Yesu, kapena akadzitchula “Khristu”?

ZOONA ZA UZIMU

1. Monga momwe Yesu anabwera koyamba pokwaniritsa maulosi, <u>Iye adzabweranso mwa mphamvu ndi ulemerero</u>. Zilipo zipembedzo zambiri zabodza, aneneri ambiri onama, ndi anthu ena odzitchula iwo okha kuti ali Mulungu. Koma pamene Yesu adzabwera kachiwiri sikudzakhala kudzadabwa kuti “Iye ndi yani?” Mawu a Mulungu anena kuti bondo lililonse lidzamgwadira Iye ndi ndi lilime lililonse lidzavomereza kuti Yesu ndi Ambuye. Aliyense amene adzabwera kwa ife namdzitchula mneneri watsopano kapena khristu watsopano kapena mulungu wina, ndiye mneneri wonama ndi wabodza.

2. <u>Yesu adzasonkhanitsa osankhidwa ake onse kuchokera kuyambira malekezero a dziko lapansi kufikira malekezero ake ena</u>.
   *Yesu analonjeza kuti abwera, ndipo anachitadi. Akulonjeza kuti adzabweranso kwachiwiri, ndipo adzabwera ndithu.
   *Pamene timuitana Yesu kuti alowe m’miyoyo yathu, nthawi imene tipereka mitima yathu kwa Iye, amalonjeza kuti sadzatisiya kapena kutitaya konse. Izi zitanthauza kuti, ngakhale tikachimwa (ndipo tonse tichimwa) Mulungu ali wokhulupirika ndi amasunga malonjezo

ake kwa ife. Palibe kanthu zimene zidzachitika nafe, kapena zimene ife tichita, ngati tapereka miyoyo yathu kwa Yesu, tidzakomana naye m'mitambo pakubwera Iye ndipo adzatitenga ife kukakhala naye kumwamba.

3. Anthu a Mulungu adzazunzidwa chifukwa cha kutsatira Iye.

Mawu a Mulungu amaphunzitsa kuti pamene dziko lili pafupi kutha, zoipa za anthu zidzakula. Adzadana koposa, adzapana koposa, ndipo adzaperekana wina ndi mnzake koposa. Mawu a Mulungu anena kuti anthu ambiri adzada iwo amene amatsatira Yesu ndipo adzawazunza. Mwina mwaonapo anthu ena akukuzunzani inu mwa njira ina yosiyana chifukwa choti inuyo mwatsimikiza mtima kutsatira Yesu. Anthu anatha kusintha maganizo awo motani kuchokera nthawi imene munasintha mtima wanu chifukwa cha kulandira Yesu? Kodi ena a iwo, ngakhale abale ndi abwenzi anu, anakudani chifukwa cha chisankho chanu chotsatira Yesu?

Mawu a Mulungu amaphunzitsa kuti tiyenera kukonda anthu amenewo.(Mateyu 5:43-48) Tiyenera kukonda iwo amene amatida ife natizunza. Tiyenera kuwakonda ndi kuwapempherera. Umo ndi m'mene Yesu anachitira iwo amene anamzunza nampereka Iye. Kukhala wotsatira wa Khristu ndi kutsata chitsanzo chake cha chikondi. Mawu a Mulungu amaphunzitsanso kuti pali dalitso lapadera losungidwira iwo ozunzika kapena ophedwa chifukwa chotsatira Yesu. Kwenikweni Mawu a Mulungu anena kuti tiyenera tiyese chimwemwe chifukwa tsiku lina tidzalandira mphoto ya zomwe tinazichita.

*Tiyeni titsirize msonkhanowu ndi pemphero. Tiyeni aliyense atigawire zimene zinachitika kuchokera mu nthawi imene tinalandira Yesu. Mwina ndi nthano yabwino ndi yokoma kapena mwina si yabwino. Kodi alipo ena ovutitsidwa chifukwa cha kutsatira Yesu? Tiyeni tipempherere anthu amenewa m'gulu lathu.

*Koma tisanapemphere, tilole aliyense amene wabwera ndi kope ndi cholembera alembe pamwamba pa pepala maina a onse amene ali m'gulu lathu. Pansi pa dzina lililonse tilembepo zoyenera kuzipempherera za wina aliyense kuti tikumbuke zonsezi. Tiyeni tilembenso ndandanda wa anthu amene timadziwa amene akusowa kuvomereza Yesu. Gawanani ndandanda umenewu ndi wina aliyense kuti tigwirizane ndi anzathu ndipo timenye nkhondo kwa abale athu anzathu amene ali otayika.

*Potuluka ife tsopano, tipempherane wina ndi mnzake tsiku ndi tsiku. Ikani pepalali m'chipinda chanu, ndipo musanagone kapena pamene mwadzuka, pempherananani wina ndi mnzake.

*Tiyeni titseke msonkhano wathu pothokoza Mulungu kuti ndiye wokhulupirika posunga malonjezo ake. Timuyamike Iye kuti anabwera pa dziko lapansi kutipulumutsa ife ku machimo athu, ndiponso chifukwa cha lonjezo lake la kubweranso kwachiwiri. Tiyeni timupemphe Iye kutithandiza ife kuti tikhale okhulupirika pa kupempherera wina ndi mnzake tsiku lililonse la sabata ino.

Kuyamba Moyo Watsopano mwa Yesu
Nkhani Zoona Zochokera mu Buku la Mateyu
Kuthawira ku Ejipito ndi Kubatizidwa Kwa Yesu
Phunziro 2, Mateyu 2-3

“Ndipo Yesu, pamene anabatizidwa, pomwepo anatuluka m’madzi: ndipo onani, miyamba inamtsegukira Iye, ndipo anapenya Mzimu wa Mulungu wakutsika ngati nkhunda nudza nutera pa Iye; ndipo onani, mawu akuchokera kumiyamba akuti, ‘Uyu ndi Mwana wanga wokondedwa, mwa Iyeyu ndikondwera.’” Mateyu 3:16,17

KUBWEREZA

1. Kodi mayi wake wa Yesu anali yani?
2. Mneneri Yesaya analosa kuti Yesu adzatchedwa “Imanuele” limene limasulidwe kutanthauza chiyani?
3. Pamene Yesu ndi ophunzira ake anali pa phiri la Azitona, Iye anawafunsa za kubweranso kwake kwachiwiri kudziko. Yesu anawauza kuti ayenera kusamala kuti asasocheretsedwe ndi ayani?
4. Yesu ananena kuti ambiri adzabwera nadzitchula iwo okha kuti ndiwo ayani?
5. Yesu anafotokozera zinthu zinayi zoopsya zimene zidzachitika padziko lonse lapansi. Kodi zinthu izi zinayi zili chiyani?
6. Yesu ananena kuti omtsatira Iye adzavutidwa. Chifukwa chiyani?
7. Yesu ananena kuti kubwera kwake kudzakhala ngati chiyani chimene chofanizira chimodzi cha zolengedwa?
8. Ndi kuti kumene angelo adzasonkhanitsa anthu ake a Mulungu?
9. Ndi yani yekha amene akudziwa tsiku limene Yesu adzabweranso?
10. Kodi ndiyenera kuchita chiyani ngati wina achita zozizwitsa zina popanda dzina la Yesu, kapena akadzitchula “Khristu”?
11. Kodi tiyenera kudziwerengera motani tikasekedwa chifukwa chotsatira Khristu?
12. Kodi ndiyenera kuwachitira chiyani iwo amene andiseka ine chifukwa chotsatira Khristu?

Yesu anabadwira ku Betelehemu nakhala kumeneko kufika pa nthawi imene anapezedwa ndi anzeru a kum’mawa. Anthu amenewo anabwera ku Israeli potsatira nyenyezi yowala. Nthawi yakungolowa m’dera la Yudeya, iwo anafika poyamba ku Yerusalemu. Kumeneko anafika kwa mfumu Herode namfunsa iye kumene mfumu yatsopano ya Israeli yabadwira chifukwa iwo anaona nyenyezi.

Herode ndi anthu onse a ku Yerusalemu anakhumudwa atamva zimenezi, choncho Herode anaitanitsa msonkhano wa chinsinsi ndi nduna zake za chipembedzo. Anawafunsa anthu ophunzirawo za zimene malembo analonjeza kuti mfumu ya Ayuda idzabadwira. Anamuuza iye kuti maulosi anafotokoza kuti Mwana ayenera kudzabadwira ku Betelehemu.

Herode anauza ophunzira kumene ayenera kupita. Koma asanachoke chinyumba chake, Herode anawafunsa kuti inali nthawi yanji imene anaona nyenyezi. Anachita izi kuti adziwe usinkhu wake wa mwanayo.

Anzeruwo anapitiriza ulendo wawo ku Betelehemu. Nyenyezi inawatsogolera ndipo inawafikitsa pa nyumba pamene Yesu anakhala. Anzeruwo analowa pa malopo namlambira Iye. Ndipo anampatsa mphatso za mtengo wapatali: golide, mure ndi lubano. Pambuyo ponyamuka kuti abwerere kupita ku mudzi kwawo, analota loto kuchokera kumwamba. M’loto limenelo anauzidwa kuti asabwerere kudzera njira ku Yerusalemu, monga momwe Herode anawafunsira, koma kuti adzere njira ina pobwerera ulendo wa kwawo.

Yosefe analota loto lina kuchokera kwa Ambuye. Loto limenelo linamchenjeza iye kuti achoke mofulumira ndi Maria pamodzi ndi mwanayo napita ku Ejipito ndi kukhala kumeneko kufikira atadzamva mawu ena ochokera kwa Ambuye. Anauzidwa kuti Herode anafuna kupha mwanayo. Izi zidzakwaniritsa ulosi umene unalosedwa m’Chipangano Chakale kuti, “Ndinaitana Mwana wanga atuluke m’Ejipito.”

Herode anachitadi chiwembu chofuna kupha mwana wolonjezedwayo. Anapha ana onse oyambira zaka zakubadwa ziwiri amene anali ku Betelehemu kapena ku madera ena ozungulira.

Pambuyo pa imfa ya Herode, Yosefe analota loto lina lomuuza kuti abwerere ku Israeli. Yosefe anamvera Mulungu. Iye anapita ku dera la kumpoto kwa Yudeya lochedwa Galileya, nakhala ku mzinda wa Nazarete.

M'masiku amenewo kunali munthu dzina lake Yohane Mbatizi amene anakhala nalalikira m'chipululu cha Yudeya. Analalikira uthenga woti, "Tembenukani mitima chifukwa Ufumu wa Kumwamba wayandikira." Yohane anavala zovala za ubweya wa mgamila, ndi lamba la chikopa. Anadya dzombe ndi uchi wa kutchire.

Anthu a Yerusalemu, Yudeya lonse, ndi dera lonse lozungulira mtsinje wa Yordani anamtulukira iye nabatizidwa mu Yordani, akuulula machimo awo. Komanso ambiri mwa atsogoleri a chipembedzo, Afarisi ndi Asaduki, anamdzera iye kuti amve mawu ake . Yohane anatchula anthuwo, "ana a njoka" chifukwa choti anakhulupirira za chipembedzo ndi miyambo kuwapulumutsa, osakhulupirira kuti ayenera kulapa machimo awo.

Pamene analalikira, Yohane analankhula za Mmodzi wina wakubwera amene adzabatiza ndi Mzimu Woyera ndi moto. Anati Mmodzi yemweyo adzapatula anthu, namsonkhaniritsa iwo omkhulupirira Iye, natumiza ena osakhulupirira kuotchedwa ndi moto wosazima.

Tsono Yesu anabwera kuchokera ku Galileya kwa Yohane ku mtsinje wa Yordani kuti abatizidwe ndi iye. Yohane anayesa kukana. Anadziwa kuti sanali woyenera. Koma Yesu anamumiriza Yohane kuti ambatize Iye kuti chilungamo chonse chikwaniritsidwe. Atabatizidwa, anatuluka m'madzi, ndipo Mzimu Woyera anatera pa Iye kuchokera kumwamba monga ngati nkhunda. Komanso mawu akulu anachokera kumwamba akunena, "Uyu ndiye Mwana wanga wokondedwa. Mwa Iyeyu ndikondwera."

MAFUNSO

1. Kodi ndi anthu otani amene anachezera Yesu atabadwa? Anampatsa Iye chiyani?
2. Poyamba, anthu amenewo anaima ku mzinda kuti? Kodi analankhula ndi yani?
3. Ndi chifukwa chiyani Mulungu anachenjeza Yosefe kuthawira ku Ejipito?
4. Kodi Yosefe anapita kuti, Herode atamwalira?
5. Kodi Yohane Mbatizi analalikira kuti?
6. Nanga Yohane anaoneka bwanji?
7. Uthenga wake wa Yohane kwa anthu unali chiyani?
8. Chinachitika chiyani ndi anthu amene analapa machimo awo?
9. Ndi chifukwa chiyani Yohane anawatchula Afarisi ndi Asaduki "ana a njoka?"
10. Yohane analalikira za Mmodzi wakubwera amene ali wamkulu kuposa iye. Anati Mmodzi yemweyo adzapatula anthu m'dziko. Izi zitanthauza chiyani?
11. Ndani anabwera kuchokera ku Galileya kubatizidwa ndi Yohane?
12. Yesu anaumiriza Yohane Mbatizi kuti amubatize Iye ngakhale anaganiza anali wosayenera. Tsono Yesu anapereka chifukwa chotani?
13. Chinachitika chiyani Yesu anatuluka m'madzi?

ZOONA ZA UZIMU

1. <u>Tikhoza kuzindikira za ubwino wa Mulungu m'miyoyo yathu pamene timumvera Iye kwathunthu</u>. Mulungu anauza Yosefe kuchita zinthu zochuluka zimene mwina sakanachita. Anamvera Mulungu namtenga Maria kukhala mkazi wake ngakhale anali ndi pakati. Iye anakhulupirira Mulungu, ngakhale sanangazindikire pakati pake. Kenaka, pamene anakhala ku Betelehemu Mulungu anawalamulira kuchoka ndi kupita ku Ejipito. Ejipito linali dziko lachilendo pamene anthu analankhula ndi chilankhulo chachilendo, ndipo anapembedza milungu yachilendo imene inali mafano. Kusintha uku kunali kovuta kwa munthu ndi banja, mkazi ndi mwana. Komabe anasankha kumvera. Motero, moyo wake wa Yesu unapulumuka.

   Monga momwe Mulungu anali ndi dongosolo lapadera pa moyo wa Yosefe, Mulungu ali ndi dongosolo lapadera kwa wina aliyense wa ife. Mawu a Mulungu amafotokoza kuti ngakhale kuyambira nthawi imene tinali m'mimba ya amayi athu, Iye anatidziwa ife

natilengera ife dongosolo lapadera lake. Tikafuna kuzindikira za ubwino umene Mulungu akufuna kuchita m'miyoyo yathu, tiyenera kumvera Iye kwathunthu. Amafuna kutitsogolera ife kuti tikhale ndi moyo wochuluka. Mawu a Mulungu akuti Mulungu akufuna kulankhula ndi wina aliyense wa ife m'mitima yathu pamene tipemphera ndi kuwerenga Mawu ake. Amachita nafe za zinthu zina zochitika m'miyoyo yathu, za makhalidwe athu, za maganizo athu. Tiyenera kusankha kuti tidzamvera Iye ngakhale tivutike. Ichi tiyenera kusankha nthawi ya mavuto isanafike.

*Kodi Mulungu akulankhula nanu za chinthu china pakati pa moyo wanu? Kodi Iye akukuuzani kuti muyenera kusintha chinthu china m'moyo mwanu chimene chili chovuta kusintha? Ngati ndi chomwecho ndi kotheka, gawanani izi m'gulu lathu. Munthu aliyense ayenera kulemba chosowachi pansi pa dzina lake m'buku limene talembamo zopempherera zathu kuti tikumbukire ndi kuti tipempherere zomwezo tsiku lililonse sabata ino. Mulungu akufuna ndipo adzakupatsani mphamvu zomvera Iye m'dongosolo lake pa moyo wanu.

2. Yesu atauka kwa akufa ndipo asanapite kumwamba, anatilamulira ife tonse omtsatira Iye lamulo. Tiyeni tibwereze mawu otsiriza a Yesu asananyamuke kupita kumwamba: "Pitani kwa anthu a mitundu yonse, mukawasandutse ophunzira anga, ndi kuwabatiza m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera; ndi kuwaphunzitsa kuti asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu. Ndipo Ineyo ndili nanu masiku onse, kufikira kutha kwa dziko lino lapansi." Patsogolo pa phunziroli tidzaphunzira njira ya kupita ndi kuuza ena za Yesu. Koma pali lamulo limodzi limene ife tonse tiyenera kuchita mwa ife tokha pomvera Mawu ake. Tiyenera kubatizidwa m'dzina la Atate ndi la Mwana ndi la Mzimu Woyera.

*Ubatizo ndi chidule cha kumvera chitsanzo chimene Ambuye Yesu anatisiyira. Uku ndi kulowa m'madzi ndi munthu wolungama wa Mulungu ndi kulola inu kupita pansi pa madzi nthawi yochepa ndi kutulukanso m'madzi.
*Yesu sanabatizidwe monga ngati kamwana. Mu Uthenga Wabwino wolembedwa ndi Luka, tiphunzira kuti Yesu anatengedwa kupita ku kachisi ali kamwana. Kumeneko wansembe anamdalitsa Iye pamodzi ndi makolo ake. Koma izi sikunena kuti ndi ubatizo.
*Yesu anabatizidwa chifukwa anasankha Iye mwini. Si chinthu chimene makolo ake anamchitira Iye ayi. M'chitsanzo cha Yesu Khristu, tonse tiyenera kupita tokha, ife eni ndi kufuna kuti tibatizidwe ndi munthu wolungama wa Mulungu.
*Ubatizo si mwambo wa chipembedzo chimene chimakuzindikiritsani kuti ndinu gulu lina lapadera kapena chipembedzo china. Si chizolowezi chimene chiyeretsa mzimu wanu ku uchimo. Koma ubatizo ndi chizindikiro chodziululira kudzipereka kwathu kutsatira Yesu. Buku Lopatulika liphunzitsa kuti ubatizo ndi chithunzithunzi cha kuikidwa ndi kuuka kwa Ambuye Yesu. Ife tikabatizidwa timadzionetsera tokha za kuikidwa ndi kuuka kwa Yesu.

Mumaganizira bwanji za Ubatizo? Kodi muganizira kuti ndi chinthu chovuta kuti mubatizidwe mwa chitsanzo cha Yesu Khristu? Kodi muyenera kubatizidwa? Kodi mukufuna kubatizidwa?

Kuyamba Moyo Watsopano mwa Yesu
Nkhani Zoona Zochokera mu Buku la Mateyu
Kuyesedwa Kwake Kwa Yesu
Phunziro 3, Mateyu 4

"Munthu sadzakhala ndi moyo ndi mkate wokha, koma ndi mawu onse akutuluka m'kamwa mwa Mulungu." Mateyu 4:4

KUBWEREZA

1. Mneneri Yesaya analosa kuti Yesu adzatchedwa "Imanuele" limene limasulidwe kutanthauza chiyani?
2. Yesu ananena kuti akadzabwera nthawi yomariza padziko adzabwera monga chiyani?
3. Yesu ananena kuti akadzabwera pa dziko, aliyense sadzasokonezeka kuti Yesu weni weniyo ndi yani chifukwa adzabwera ndi mphamvu ndi ulemerero pobwera pa chiyani?
4. Yesu ananena kuti Iye asanafike anthu ambiri adzachita zodabwitsa zina nadzionetsera ngati Khristu. Tiyenera kuchenjeza kuti aneneri onyengawa asatichitire ife chiyani?
5. Yesu ananena kuti tidzaganizira chiyani ife tokha pamene ena atida chifukwa chotsatira Iye? Anatinso kuti sitidzataya mphoto yathu, ndiponso tiyenera kuwachitira chiyani anthuwo amene amatida?
6. Yesu ananena kuti ndi yani yekha amene akudziwa tsiku limene Iye adzabweranso?
7. Munthu amene anakhala m'chipululu nalalikira uthenga wa kulapa navala zovala za chikopa cha ngamila nadya dzombe ndi uchi kutchire anatchedwa dzina lake ndani?
8. Anthu ambiri amene anadza kubatizidwa ndi Yohane, iwo analapa chiyani?
9. Yohane ananena kuti Mmodzi akubwera amene adzapatula anthu a pa dziko lapansi, ndipo kuti iwo amene amukana Iye adzatsutsidwa naponyedwa kuti?
10. Yesu anadza kwa Yohane nampempha iye kuti amuchitire chiyani?
11. Pa ubatizo wa Yesu ndani anatsika kuchokera kumwamba natera pa Iye? Nanga mawu ochokera kumwamba anali a yani?
12. M'mawu ake otsiriza asanapite kumwamba, Yesu anauza ophunzira ake kuti ayenera kutchita chiyani ndi iwo amene amulandira Iye monga Ambuye ndi Mpulumutsi.
13. Kodi ubatizo ukhoza kutiyeretsa ife ku machimo athu? Ubatizo ndi chizindikiro chotionetsera ife ndi chiyani?
14. Kodi ubatizo umafanizira zochitika zitatu ziti m'moyo mwa Yesu?

Yesu atabatizidwa, Mzimu Woyera anamtsogolera Iye kuchipululu kumene anayesedwa ndi Satana. Yesu anakhala kumeneko masiku makumi anayi usiku ndi usana wosadya. Patapita masiku amenewo Yesu anali ndi njala. Nthawi yomweyo Satana anadza naye nanena, "Ngati muli Mwana wa Mulungu, tauzani kuti miyala iyi isanduke mikate." Koma Yesu anamuyankha iye pogwiritsa ntchito Malembo m'Chipangano Chakale nati, "Kwalembedwa, 'Munthu sadzakhala ndi moyo ndi mkate wokha, koma ndi mawu onse akutuluka m'kamwa mwa Mulungu."

Pambuyo pake Satana anatenga Yesu kupita naye ku Yerusalemu namuika Iye pa nsonga ya kachisi nanena naye, "Ngati muli Mwana wa Mulungu, mudzigwetse nokha pansi: pakuti kwalembedwa, 'Adzalamula angelo ake kuti akusamaleni, ndipo pa manja awo adzakunyamula kuti mapazi anu angapweteke pa miyala.'" Yesu anamuyankhanso ndi Malembo nati, "Kwalembedwanso kuti usamuyese Mulungu wanu."

Pomwenso Satana anatenga Yesu napita naye ku phiri lalitali, namuonetsa Iye maiko onse a dziko lapansi ndi ulemerero wawo. Ndipo Satana ananena kwa Iye, "Zonsezi ndidzakupatsani mukandigwadira ine." Pomwepo Yesu anamuuza iye, "Choka Satana, pakuti kwalembedwa, 'Ambuye Mulungu wako udzamgwadira, ndipo Iye yekha yekha udzamlambira." Satana anamvera Yesu namusiya. Angelo anabwera kudzamtumikira Yesu.

MAFUNSO

1. Kodi Mzimu Woyera anamtenga Yesu ku malo ati kuti ayesedwe ndi Satana?
2. Kodi Yesu anachita chiyani masiku makumi anayi usana ndi usiku asanayesedwe ndi Satana?
3. M'mayesero awiri oyamba, Satana anauza Yesu kusonyeza kuti Iye ndi yani?
4. Mu yesero loyamba, Satana anafuna Yesu kuti asandutse miyala kukhala chiyani?
5. Kodi Yesu anapambana Satana bwanji mu yesero loyamba?
6. Mu yesero lachiwiri Satana anamyesa Yesu kuti achite chiyani atafika pa nsonga ya kachisi m'Yerusalemu?
7. Kodi Yesu anapambana Satana bwanji mu yesero lachiwiri?
8. Mu yesero lachitatu Satana anamlonjeza Yesu kuti adzampatsa Iye maufumu onse a pa dziko lapansi ngati Iye adzamchitira chinthu chimodzi. Kodi Satana anafuna kuti Yesu amuchitira iye chiyani?
9. Kodi Yesu anapambana Satana bwanji mu yesero lachitatu?
10. Ndani anabwera kudzamtumikira Yesu atamchotsa Satana?

ZOONA ZA UZIMU

1. <u>Tonse tidzakumana ndi mayesero, ngakhale titapereka miyoyo yathu kwa Yesu</u>. Mawu a Mulungu amaphunzitsa kuti timayesedwa osati ndi Satana yekha, komanso chifukwa cha zilakolako zathu (Yakobo 1:14). Amaphunzitsanso kuti mkati mwa mitima yathu muli nkhondo chifukwa cha zilakolako zofuna kuchita zabwino ndi zilakolako za kuchita zoipa. "Pakuti chimene ndikuchita sindichidziwa; pakuti sindimachita chimene ndikufuna, koma chimene ndimadana nacho ndikuchita ichi…Pakuti chabwino chimene ndimachifuna, sindikuchita; koma choipa chimene sindimachifuna, chimenecho ndikuchichita." Aroma 7:15,19

2. <u>Mudzakumana ndi mayesero chifukwa tsopano muli ndi maonekedwe mwa inu</u>. Kaonekedwe koyamba ndi ka thupi ndipo kena ndi ka mzimu wa Mulungu (Mzimu Woyera) mwa inu. Mu Agaliteya 5:16,17 tiwerenga kuti, "Muyendeyende ndi Mzimu, ndipo musafitse chilakolako cha thupi. Pakuti thupi lilakalaka potsutsana naye Mzimu; ndi Mzimu potsutsana nalo thupi; pakuti izi sizilingana; kuti zimene muzifuna musazichite." Kudzakhala nkhondo pakati pa zofuna zathu zimasemphana ndi zifuniro za Mulungu mwa zazikulu kapena zazing'ono za moyo wathu.

3. <u>Tikhoza kupambana mayesero monga momwe Yesu anachitira, kupyolera mwa mphamvu ya Mawu a Mulungu</u>. Mu Ahebri 4:12 tiwerenga kuti, "Pakuti Mawu a Mulungu ali a moyo, ndi ochitachita, ndi akuthwa koposa lupanga lakuthwa konse konse, napyoza kufikira kugawira moyo ndi mzimu, ndi zimfundo ndi mafuta a m'mafupa, nazindikiritsa zolingirira ndi zitsimikizo za mtima." *Werengani ndime imeneyi koposera kamodzi. Funsani anzanu kukuuzani zimene iwo akuganizira zimene ndimeyi itanthauza*.

<u>Mawu a Mulungu si buku monga la malangizo. Ndi Mawu a moyo amene Mulungu amalankhula m'mitima yathu mu njira ya pa yekha. Amalowa mkati mwa moyo m'mene Mulungu yekha amadziwa.</u>

Chinthu chimodzi chopambana chimene otsatira Yesu aliyense ayenera kuchita ndi kukhala ndi nthawi tsiku lililonse ndi Atate. Satana akhoza kuchita chilichonse angathe kuti akuchotseni pa Mawu ake a Mulungu chifukwa amadziwa kuti Mawu ake ndi gwero lamphamvu. Akhoza kutiuza ife kuti tili otanganidwa; kuti taphunzira kale Mawu a Mulungu; kuti tiyenera kugona, kuti Mawu a Mulungu ndi ovutilapo kuti tilimvetsetse, kapena zidandaulo zina zochuluka. Koma kwenikweni tiyenera kuzindikira kuti maganizo amenewo ndi bodza. Tiyenera kukhala ndi nthawi yokhala ndi mapemphero a tsiku lililonse a Mawu a Mulungu.

Ili ndi dongosolo losavuta kulitsata:

1. Yambani nthawi yanu ya pa nokha ndi Mulungu kumuuza Iye m'mene inuyo mumam-kondera Iye ndi kumthokoza Iye pa zopambana zonse monga momwe Iye alili.
2. Kuthokoza Iye pa zonse zimene Iye wachitira m'moyo mwanu, kapena mayankho onse a mapemphero amene inuyo mwapemphedwapo.

*Ndi bwino kukhala ndi tsamba limodzi kapena chigawo chimodzi mu kope lanu lotchedwa, "Zothokoza" ndi kulemba zinthu zimene Mulungu akuchita m'moyo mwanu. Nthawi zonse lembani tsiku. Mwa njira imeneyi mukhoza kusungira zimene Mulungu akuchita m'moyo mwanu.

3. Kupempherera anthu ena: Iwo amene ali m'gulu lanu lophunzira Mawu a Mulungu, abale anu, abwenzi anu, makamaka iwo amene sanamdziwe Yesu mpaka tsopano, ndi zosowa zapadera. Ngati muli ndi anthu ambiri ochuluka oyenera kuwapempherera, muyenera kukhala ndi tsamba lonse lathunthu kapena chigawo chilichonse tsiku lililonse pa sabata ndi kugawa anthu a pa banja lanu ndi abwenzi anu pa kuwapempherera kamodzi pa sabata. Mwa chitsanzo:

Lolemba	Lachiwiri	Lachitatu	Lachinayi (ndandanda…)
Bambo	Agogo	Mbusa Phiri	Azimayi amvano
Mayi	Apongozi Banda	Atumiki a mpingo	Aphunzitsi
Chisomo	Samueli	Aakulu a konvenshoni	Mayi Ngozo
Sitivini	Malume Chisale	Bambo Nyirenda	
Tomasi			

*Tiyeni tichite ichi pamodzi kuti aliyense adzatha kuyamba nthawi yopemphera yake ya pa yekha mosayembekezera kuchichita pomwepo.

4. Kuwerenga ndi kuganizira za Mawu a Mulungu. Mawu a Mulungu amaphunzitsa kuti sitiyenera kungowawerenga chabe monga ngati tiwerenga mabuku ena, koma tiyenera kuwalingirira Mawuwo. Izi zitanthauza kuti tiyenera kuchita izi:
   *Kuwerenga pang'onopang'ono.
   *Kuwerenganso kambirimbiri ndi kuganizira mozama mu tanthauzo la mawu. Izi zikhoza kutitengera nthawi kuwerenga zinthu zochuluka tisanafike polingirira pa choonadi cha Mulungu kuti tithe kupitirira.
   *Gwiritsani ntchito dzina lanu la inu eni pa choonadi cha Mawu. Mwa chitsanzo, ngati ndime ikunena, "Lemekeza atate ndi amayi ako…" Ikani dzina lanu mkatimo, monga ngati ichi: "Davide, uyenera ku lemekeza atate ndi amayi ako."
   *Pempherani ndimeyi monga pemphero lanu kwa Mulungu ndi kumthokoza Iye pa madalitso ake ndi kumpempha Iye zosowa zanu. Mwa chitsanzo, "Zikomo Atate chifukwa cha atate ndi amayi anga. Ndikuthokozani kuti Inu ndinu Atate wanga wa kumwamba amene mumakwaniritsa zosowa zanga."

Mawu a Mulungu ali ndi zoonadi zambiri zimene Mulungu akufuna alankhule kwa ife pa moyo wathu nthawi ino. Ichi ndi chitsanzo cholingirira Mawu a Mulungu:

*Tiyeni tiyambe ndi mutu wachisanu wa Mateyu. *Tiyeni timpatse munthu aliyense mpata wa kuwerenga ndime zitatu kapena zinayi. Ngati wina akulephera kuwerenga, mtsogoleri ayenera kuwerenga ndime zake nthawi zonse kopanda kufotokozera*.

*Tiyeni aliyense ayese kuganizira tanthauzo la ndimezi, ndipo muike dzina lanu pa ndime pamene nkotheka. Musachite mantha pakulola Mzimu wa Mulungu kukulankhulani inu. Ichi ndi chitsanzo, koma si njira yokhayo imene ndimeyi ikhoza kukhala m'moyo mwake mwa munthu. Awa ndi mawu amene Ambuye analankhula ndi ine nditaziwerenga ndimezi.

Ndime 3: “Odala ali osauka mu mzimu; chifukwa uli wawo Ufumu wa Kumwamba.”

(Chitsanzo cha “choonadi cha uzimu” cha mlembi wa nkhaniyi) - Ndime 3…Ndili wodalitsidwa ngati ndili wosauka mu mzimu., chifukwa ndidzalandira cholowa ku Ufumu wa Mulungu. Ambuye, ndithandizeni ine kukhala wosauka mu mzimu. Sindikufuna kukhala wodzitama, wonyada ndi wodzadza ndi mzimu wa ine mwini. Zikomo Ambuye chifukwa ndikudziwa kuti ndidzalandira Ufumu wa Mulungu. Nditsimikizira kuti ndili munthu wodalitsidwa.

Ndime 4: “Odala ali a chisoni; chifukwa adzasangalatsidwa.”

(Chitsanzo cha “choonadi cha uzimu” cha mlembi wa nkhaniyi) – Ndime 4…Ndi chinthu chovuta kwa ine kudalitsidwa mu nthawi ya chisoni, chifukwa nthawiyi ndi nthawi yosakondwa. Koma pakuti ndine wotsatira wake wa Yesu, ndikuthokoza chifukwa ndikudziwadi kuti ndadalitsidwa. Pakuti pali chiyembekezo kwa ife okhulupirira Yesu. Mulungu amatipatsa ife chiyembekezochi ndipo m’menemo chititonthoza. Ambuye zikomo pokhala wonditonthoza nthawi ya chisoni changa mu nthawi ya imfa ya mayi wanga. Ndikuthokozani chifukwa cha anthu amene munandipatsa amene ananditonthoza mu nthawi yanga ya chisoni. Zikomo chifukwa cha chitonthozo ndinachilandira kuchokera kwa Mzimu Woyera m’moyo mwanga. Inde, Ambuye, ndikuona kuti ine, monga wokhulupirira, ndili dalitsidwa nthawi ya chisoni.

Kulibe njira yapadera, kapena mawu apadera. Chofunika ndi kulingirira Mawu a Mulungu. Lolani kuti azame m’moyo mwanu. M’menemo, Mulungu adzalankhula m’katikati mwa moyo wanu wonse.

Pochita zimenezi mowirikiza, timakhala monga ngati Yesu mu njira zonse. Tidzatha kuima pa mayesero, komanso tidzaonetsa chikondi choposa ndi khalidwe la Mulungu m’magawo onse a miyoyo yathu. Kumudziwa Mulungu m’miyoyo yathu ndi maziko opambana a moyo wathu.

*Ndikulimbikitsani kuti mugawe mapeto a kope lanu. Gawo ili lidzakhala la kulingirira. Lembani tsiku nthawi zonse pamene mutsegula Mawu a Mulungu ndi kulemba zinthu zimene Mulungu akulankhulirani inu. Nthawi zina ndi chosavuta kulingirira pa Mawu a Mulungu pakulemba maganizo anu. Nthawi zina mwina mudzafuna kubwerera mbuyo ndi kuwerenga zimene Ambuye akulankhula ku mtima wanu. Iyi ndi nthawi yapadera kwa inu ndi Mbuye wanu.

*Ndikutsimikizirani inu kuti mudzipereka nokha ndi gulu lanu kwa sabata limodzi, kuti mudzakhala wokhulupirika kukhala ndi nthawi ndi Atate kwa mphindi khumi ndi zisanu tsiku lililonse. Ngati nkotheka, lembani chinthu chimodzi chimene Mulungu alankhula ndi inu tsiku lililonse. Ngati simudziwa kuwerenga, onetsetsani kuti mupeze wina kuti akuwerengereni ngakhale ndime imodzi pa tsiku sabata ino. Pa sabata likubweralo onani zimene zidzachitika pamene Mawu a Mulungu aloledwa azame m’mtima mwanu tsiku ndi tsiku.

*Tiyeni tonse tipitirize kuwerenga ndime zimene tinayambazo. Sikuyenera kuchita changu kumaliza mwa tsiku limodzi. Mutawerenga mutu umodzi m’Mawu a Mulungu, mungopitiriza ndi mutu wina. Nthawi ina tiyeni tigawane zimene tapeza ndi kulingirira za Mawu ake a Mulungu.

Kuyamba Moyo Watsopano mwa Yesu
Nkhani Zoona Zochokera mu Buku la Mateyu
Kuthetsa Mantha Kwa Asodzi a Anthu
Phunziro 4, Mateyu 4-8

“Ndipo ananena Iye kwa iwo, ‘Muli a mantha bwanji okhulupirira pang’ono inu? Pomwepo Iye anauka, nadzudzula mphepo ndi nyanja, ndipo panagwa bata lalikulu.” Mateyu 8:26

*Inu monga mtsogoleri, kumbukirani kufunsa gulu lanu ngati anatha kuwerenga m’Mawu a Mulungu ndi kupemphera tsiku lililonse. Patsani mwayi wina aliyense kufotokozera zimene akumana nazo. Alimbikitseni zimene achita.

*Chifukwa cha mtundu wa phunziro la sabata ino, ndi chinthu chofunikira kupereka nthawi yokwanira kupempherera zosowa ndi kupempherera poyamba pa phunziro, osati pomaliza.

KUBWEREZA

1. Mneneri Yesaya analosa kuti Yesu adzatchedwa “Imanuele” limene limasulidwe kutanthauza chiyani?
2. Pa phiri la Azitona Yesu anaphunzitsa ophunzira ake za kubwera kwake kw achiwiri. Yesu anawauza iwo kuti anthu ambiri adzachita zodabwitsa zina nadzionetsera ngati Khristu ndipo ayenera kuchenjera kuti aneneri onyengawa asawachitire iwo chiyani? Yesu ananena kuti akadzabwera nthawi yomariza padziko adzabwera monga chiyani?
3. Yesu ananena kuti akadzabwera kachiwiri pa dziko, aliyense adzamuona Iye kubwera ndi mphamvu ndi ulemerero waukulu? Kodi adzaoneka kuti?
4. Yesu ananena kuti ndi yani yekha amene akudziwa tsiku limene Iye adzabweranso?
5. Munthu amene anakhala m’chipululu nalalikira uthenga wa kulapa navala zovala za chikopa cha ngamila nadya dzombe ndi uchi kutchire anatchedwa dzina lotani?
6. Yohane anabatiza anthu ambiri amene anadza kwa iye m’chipululu. Kodi iwo analapa chiyani?
7. Yesu asananyamulidwe kumwamba, kodi analamulira kuti omtsatira Iye ayenera kuchita chiyani?
8. Yohane ananena kuti Mmodzi akubwera amene adzapatula anthu a pa dziko lapansi, ndipo kuti iwo amene amukana Iye adzatsutsidwa naponyedwa kuti?
9. M’mayesero awiri oyamba, Satana anauza Yesu kusonyeza kuti Iye ndi yani?
10. Yesu anayankha Satana katatu pogwiritsa ntchito chiyani?
11. Ngati timafuna kumudziwa Mulungu bwino, ndi chofunikira kuti tichite chiyani ndi Iye tsiku ndi tsiku?
12. Kodi ndi makhalidwe awiri ati amene ali ndi nkhondo mwa inu?
13. Ngati timafuna kupambana mayesero ndi chofunikira kuti tikhale ndi nthawi ya patokha ndi ndani tsiku lililonse?
14. Tikafuna kufanana ndi Yesu, ndi chofunikira kukhala ndi nthawi ya patokha naye bwanji?

Yesu anayamba utumiki wake poyera atabwerera kuchokera ku chipululu. Iye anakhala ku dera lozungulira nyanja la Galileya, ku mzinda wa Kapernao. Komweko analalikira uthenga womwemo wolalikiridwa ndi Yohane Mbatizi, kuti, “Lapani, chifukwa Ufumu wa Mulungu wayandikira!”

Ophunzira awiri oyamba oitanidwa ndi Yesu anali Simoni Petro ndi Andreya. Abale awiri amenewo anali pamodzi kuponya makhoka awo m’nyanja ya Galileya kupha nsomba. Yesu anawaitana nati, “Tsatani ine ndipo ndidzakusandutsani inu kukhala asodzi a anthu.”

Kuchokera kumeneko, Iye anapitiriza nafika kwa munthu ndi ana amuna ake awiri amene anakhala m’bwato lawo akukonzanso makhoka awo. Yesu anaitana amenewo kumtsatira Iye. Maino awo anali Yakobo ndi Yohane, ndipo dzina la bambo wawo anali Zebedeo.

Tsono Yesu anapita nazungulira m’dera lonselo naphunzitsa m’nyumba zopemphere-ramo za Chiyuda. Analalikira uthenga wabwino wa Ufumu wa Mulungu nachiritsa matenda

osiyanasiyana. Mbiri yake inakula kwambiri ngakhale anthu ena ozungulira ku dziko lina la Siriya anadza kwa Iye kudzachiritsidwa.

Yesu ataona anthu ambiriwa kumlondola Iye, anatenga ophunzira ake napita ku phiri. Kumeneko Iye anakhala pansi nayamba kuwaphunzitsa ophunzira ake zinthu zambiri za Ufumu wa Mulungu.

Anthu anamvera ziphunzitso za Yesu ndipo anazizwa ndi ulamuliro umene anali nawo. Sanayambe kumva munthu kuwaphunzitsa kotero ngakhale m'nyumba zopemphereramo zawo za iwo eni.

Pamene Yesu anatsika pa phiri, khamu lalikulu linalipo kale kumyembekezera Iye ndi kumtsatira Iye kulikonse kumene Iye amapite. Mkati mwawo munali wina wakhate, ndipo anamupempha Yesu ngati angalole kuti amuchiritsa nthenda yake. Posachedwa munthu uja anachiritsidwa. Munthu wina, msirikali wa Chiroma anampempha Yesu kuti achiritse mnyamata wake wopuwala amene anali kugona kunyumba. Yesu anamchiritsa.

Yesu anapita ku nyumba ya Simoni Petro chifukwa mpongozi wake wa Petro anadwala malungo ndipo anadwala kwambiri. Yesu anagwira dzanja lake ndipo malungo onse anamchokera iye. Mpongoziyo anadzuka natumikira wina aliyense m'nyumbamo.

Yesu anakhala komweko madzulo onse ndipo anachiritsa anthu nachotsa ziwanda zambiri. Koma nthawi imene anaona khamu lalikulu lomzungulira Iye pa malopo, analamula ophunzira ake kuti apite naye kutsidya lina la nyanja ya Galileya.

Inali kale nthawi yotayika usiku pamene Yesu ndi ophunzira ake analowa m'galawa kuti awolokere tsidya lina la nyanja. Koma posakhalitsa nthawi, pokhala iwo pakati pa nyanja, mphepo yayikulu inabwera ndipo mafunde anavutitsa bwato. Ophunzira ake a Yesu, ngakhale ambiri anali asodzi ozolowera ndi nyanja, anadziwa choopsya chimene anakomana nacho, ndipo anagwidwa ndi mantha akulu. Koma Yesu anali m'tulo ndipo sanadzuke.

Ophunzira anaopsedwa, nadzutsa Yesu nanena, "Ambuye, tipulumutseni ife! Tili kutayika!" Yesu anawayankha iwo, "Chifukwa chiyani muli kuopa, inu a chikhulupiriro chochepa?" Ndipo iye anauka naimilira natontholetsa mphepo ndi nyanja, ndipo kunali bata lalikulu. Ophunzira anazizwa ananena, "Kodi ameneyu ndi yani, kotero ngakhale mphepo ndi nyanja zimumvera Iye?"

MAFUNSO

1. Kodi unali uthenga wotani umene Yesu analalikira kwa anthu?
2. Kodi maina a ophunzira awiri oyamba a Yesu anali ayani?
3. Kodi ntchito ya ophunzira ake ambiri a Yesu inali yotani?
4. Ndi chifukwa chiyani anthu ochuluka anabwera kudzaona Yesu?
5. Ndi chifukwa chiyani otsatira ake a Yesu anazizwa ndi ziphunzitso zake pamene anali pa phiri?
6. Yesu atatsika pa phiri, anachiritsa munthu wodwala nthenda yotani?
7. Yesu anachiritsanso mnyamata wa msirikali wa Chiroma. Kodi iye anadwala chiyani?
8. Yesu anachiritsa mmodzi wa abale ake a Simoni Petro. Kodi ameneyo anali ndani?
9. Ndi chifukwa chiyani Yesu anafuna kuwolokera ku tsidya lina la nyanja ya Galileya?
10. Kodi Yesu anachita chiyani m'galawa?
11. Ndi chifukwa chiyani ophunzira ake a Yesu anachita mantha?
12. Ndi chifukwa chiyani Yesu anawatsutsa ophunzira ake?
13. Kodi ophunzira ake a Yesu ananena chiyani atamuona Yesu kuti aletsa namondwe?

ZOONA ZA UZIMU

1. <u>Yesu akuitana ife tonse kukhala "asodzi a anthu</u>." Yesu amatilamulira ife kugawana ufulu umene tili nawo mwa Iye ndi anthu onse: m'maiko onse, m'mizinda yonse ndi m'midzi yonse pa dziko. Awa anali mawu ake otsiriza amene analankhula kwa ophunzira ake asanabwerere kumwamba. Pa phunziro lotsiriza la maphunzirowa tidzaphunzira njira zimene tingagawire chikhlulpiriro chathu cha Yesu momveka kwa anthu ena. Nthawi zina timaganiza kuti, "Ine ndine yani? Ndilibe maphunziro ochuluka. Nanga ndingachite chiyani kukopa wina kuti atsatire Yesu? Ndipo ngati ndingathe, popeza ndikukhala m'gawo lina laling'ono la dziko lapansi, nanga Yesu akhoza bwanji kundigwiritsa ntchito ine kusintha maiko ena?

Mawu a Mulungu amaphunzitsa kuti ngakhale ndikadakhala mlaliki wabwinodi wopambana wina aliyense, sindidzatha kukopa wina kumtsatira Yesu. Pamene tinapereka miyoyo yathu kwa Yesu, sanali munthu amene anatizindikiritsa, koma anali Mzimu Woyera wa Mulungu amene anatifikitsa pa kulapa. Mu Yohane 16:8 tiwerenga kuti, “Atadza Iyeyo, adzatsutsa dziko lapansi za machimo, ndi za chilungamo, ndi za chiweruziro.”

Udindo wathu monga asodzi a anthu ndi kugwira “makhoka a moyo wathu” ndi kulowetsa “nsomba” zonse zimene Mzimu Woyera amatibweretsera kwa ife.

Khwerero loyamba la kugawira chikhulupiriro chathu ndi ena ndi kunena zimene Yesu amachita m’miyoyo yathu. Njira imeneyi ya kugawana imatchedwa “umboni.” Liwu lakuti “umboni” ndi liwu limene limagwiritsidwa ntchito ku bwalo la milandu. Mboni zimanena zinthu zimene iwo akudziwa kuti ndi zoona kapena zinthu zimene iwo anaona pamene zinachitika. Anthu akhoza kutsutsana kuti inu ndinu wozungulira mutu, kapena kuti ndinu mboni yoipa, koma sangatsutsane ndi zimene zachitika patsogolo pamaso panu. Tiyeni tichite ntchito iyi limodzi:

-Lolani munthu aliyense kuganizira mbuyo m’mene iye moyo wake unalili asanadziwe Yesu.
-Ganizirani m’mene Yesu anadziwika kwa inu.
-Ganizirani za nthawi Mzimu Woyera analankhula m’mtima mwanu ndi m’mene munadziwa kuti Yesu ndi Mulungu ndipo munamsowa Iye m’moyo mwanu.
-Ganizirani za kusankha kwa moyo wanu podzipereka kwa Yesu.
-Potsiriza, ganizirani zimene Yesu anasinthira m’moyo mwanu.
-Pambuyo poganizira zimenezi, tilole munthu aliyense m’gulu lathu kuchita umboni wake ndi gulu. NDI CHINTHU CHOFUNIKA KUTI MUSATENGE NTHAWI YOPOSA MPHINDI ZITATU.

*Komanso ndi nthawi ino, monga ngati gulu, tiyambe kulimbikitsana wina ndi mnzake mu nthawi yathu yapadera ya patokha pakupempherera iwo amene Mulungu wationetsera ife kuti ali kusowa kuvomereza Iye. Mwina akhoza kukhala anthu ena ku sukulu kapena ku malo ogwirira ntchito. Mwina ali abale athu amene sanalandire Yesu. Pempherani limodzi chifukwa cha anthu amenewa. Wina aliyense m’gulu lathu alembe mu kope lake maina amene atchulidwa ndi gulu. Tiyenera kugwira ntchito limodzi kubweretsa anthu onse kwa Yesu.

*Koma tisaiwalire anthu ena amene amakhala kutali ndi ife. Ndi udindo wathu kuwapem-phereranso anthu amenewo.
**Ganizo la kwa mtsogoleri wa gulu: Mwina inu kapena mbusa wanu amadziwa wamishoni wina amene amakhalira ku dziko lina kapena ku dera lina la dziko lathu. M’gulu lanu pemphererani munthuyo, ndi banja lake, ndiponso anthu amene amawatumikira. Chitani zimenezi m’gulu lanu sabata iliyonse nthawi imene mupempherera anthu ena. Pezani wina wake pa gulu lanu kulembera wamishoniyo kumfunsa iye zosowa zake ndi zinthu zina zopempherera. Pempherani ndi kufufuza njira zimene gulu lanu likhoza kuthandiza kugawa Uthenga Wabwino wa Yesu kwa anthu amene ali kutali ku dziko lapansi. Imani ndi kukambi-rana zimenezi tsopano musanayambe kuona choonadi china chachiwiri*.

2. Yesu anadzudzula ophunzira ake, sikuti chifukwa anamdzutsa Iye kutontholetsa namondwe ayi, koma chifukwa choti anagwidwa ndi mantha. Ophunzira ake anayang’ana namondwe. Anali anthu amene anazolowera ndi mphepo ndipo anazindikira kuti mphepo imeneyo inali yoipa. Chimene iwo sanazolowere chinali mphamvu yake ya Mulungu m’miyoyo yawo. Sanazindikire kuti Mulungu ndi wamkulu kuposa mavuto awo, ndipo Iye anakhala nawo limodzi m’bwato.

Ine ndili ndi mwana amene ali ndi chaka chimodzi ndi theka amene wayamba kufufuza zinthu zomzungulira iye. Nthawi yina mwanayo anaopa galu amene anabwera kwa iye. Anathawira kwa ine ndipo ndinamnyamula iye m’manja mwanga. Posakhalitsa analeka kuopa chifukwa anadziwa kuti ndimamkonda iye, ndipo anandikhulupirira ine kumsamalira iye.

Ife tili ana a Mulungu kuyambira nthawi imene tipereka miyoyo yathu kwa Iye. Iye ndi mtetezi wathu. Amatisamalira ife. Amatikonda, ndipo pamene tikuopa tiyenera kuthawira kwa Iye. Pokhala ife m’manja mwa Ambuye ndi kumvera Iye, amatichotsera mantha.

M’Chipangano Chakale kunali munthu dzina lake Davide. Iye anapyola mu zinthu zovuta zambiri chifukwa mfumu Sauli anafuna kumupha iye. Atangozindikira Davide zoonadi za Mulungu nakula pokhala pafupi ndi Iye, analemba ndakatulo zambiri zotchedwa, “Masalimo.” Izi ndi ndakatulo zimene zinauzililidwa ndi Mulungu kuphunzitsa za Mulungu. Muli masalimo okwanira zana limodzi makumi asanu, si onse olembedwa ndi Davide, koma akupezeka m’Chipangano Chakale. Davide analemba masalimo ena onena za mantha, koma ndasankha salimo limodzi kuti tiwerenge ndi kulingirira m’sabata imeneyi: Salimo 27. Werengani Salimo limeneli mu nthawi yanu ya kulankhula ndi Mulungu. Ngati mulibe buku la Chipangano Chakale, ndakulemberani Salimo limeneli m’maphunziro amenewa. Pemphani Mulungu kukuphunzitsani kuti muike mantha anu onse ndi kukhala m’manja ake a chikondi ndi chitetezo.

*Tsekani phunziro lino ndi pemphero, koma nthawi ino, wina aliyense akhale ndi mnzake amene angamukonde wofanana naye. Yankhulani wina ndi mnzake pa zinthu zina zazikulu zimene mumachita nazo mantha. Pemphereranani pa zinthu zimenezi, ziperekeni pamaso pa Mulungu kuti akchotsereni mantha ndi kuikapo chikhulupiriro kwa Iye. Uzani Mulungu zofuna zanu kuti mudalire Iye, ngakhale zinthu zina zimene zimakuopysezani.

Salimo 27

Chauta ndiye kuunika kwanga ndi chipulumutso changa; ndidzaopa yani?
Chauta ndiye mphamvu za moyo wanga; ndidzacita mantha ndi yani?

Pondifike ine ochita zoipa kudzadya mnofu wanga,
Inde akundisandutsa ndi adani anga, anakhumudwa iwo nagwa.

Lingakhale gulu la ankhondo limanga misasa kuti andithyole,
Mtima wanga sungachite mantha:
Ingakhale nkhondo ikandiukira,
Inde pomweponso ndidzakhulupirira.

Chinthu chimodzi ndinachipempha kwa Chauta, ndidzachilondola ichi:
Kuti ndikhalitse m’nyumba ya Chauta masiku onse a moyo wanga,
Kupenya kukongola kwake kwa Chauta ndi kufunitsa m’Kachisi mwake.

Chifukwa kuti pa dzuwa la tsoka Iye adzandibisa mumsasa mwake:
Adzandibisa m’tsenjezi mwa chihema chake;
Pathanthwe adzandikweza.

Ndipo tsopano mutu wanga udzakwezeka pamwamba pa adani anga akundizinga;
Ndipo ndidzapereka m’chihema mwake nsembe za kupfuula mokondwera;
Ndidzayimba, inde, ndidzayimbira Chauta zomlemekeza.

Imvani, Chauta, liwu langa popfuula ine:
Mundichitirenso chifundo ndipo mundivomereze.

Pamene munati, Funani nkhope yanga; mitma wanga unati kwa Inu:
Nkhope yanu, Chauta, ndidzafuna.

Musandibisire ine nkhope yanu;
Musachotse kapolo wanu ndi kukwiya:
Inu munakhala thandizo langa;
Musanditaye, ndipo musandisiye Mulungu wa chipulumutso changa.

Pakuti wandisiya atate wanga ndi amayi wanga,
Koma Chauta anditola.

Mundiphunzire njira yanu, Chauta,
Munditsogolere pa njira yachidikha, chifukwa cha adani anga.

Musandipereke ku chifuniro cha akundisautsa:
Chifukwa zinandiukira mboni zonama ndi iwo akupumira za chiwawa.

Ndikadapanda kukhulupirira kuti ndikaone ubwino wa Chauta
M’dziko la amoyo, ndikadatani!

Yembekeza Chauta:
Limbika, ndipo Iye adzalimbitsa mtima wako;
Inde yembekeza Chauta.

Kuyamba Moyo Watsopano mwa Yesu

Nkhani Zoona Zochokera mu Buku la Mateyu

Chikondi –Tanthauzo Lake la Utumiki wa Yesu pa Dziko Lapansi

Phunziro 5, Mateyu 8-10

“Koma Iye, poona makamuwo, anagwidwa m’mtima ndi chisoni chifukwa cha iwo, popeza anali okambululudwa ndi omwazikana, akunga nkhosa zopanda mbusa.” Mateyu 9:36

*Musanayambe phunziro ili, fufuzani ndi anthu angati amene akhala ndi nthawi yawo yapadera ndi kulankhula ndi Ambuye. Koma simuyenera kukhala wovuta, koma mwa chikondi limbikitsanani wina ndi mnzake kuti akhale m’Mawu a Mulungu tsiku lililonse. Alimbikitseni kupitiriza kupempherera anthu amene anatchulidwa kuti akusowa Yesu. Onani ngati ena anapeza nthawi ya kugawana za umboni wawo sabata ino.

KUBWEREZA

1. Mneneri Yesaya analosa kuti Yesu adzatchedwa “Imanuele” limene limasulidwe kutanthauza chiyani?
2. Yesu ananena kuti akadzabwera kwachiwiri pa dziko, aliyense adzamuona Iye kubwera ndi mphamvu ndi ulemerero waukulu? Kodi adzaoneka kuti?
3. Yesu ananena kuti ndi yani yekha amene akudziwa tsiku limene Iye adzabweranso?
4. Yohane anabatiza anthu ambiri amene anadza kwa iye m’chipululu. Kodi iwo analapa chiyani?
5. Yohane ananena kuti Mmodzi akubwera amene adzapatula anthu a pa dziko lapansi, ndipo kuti iwo amene amukana Iye adzatsutsidwa naponyedwa kuti?
6. Yesu anayankha Satana katatu pogwiritsa ntchito chiyani?
7. Ngati timafuna kumudziwa Mulungu bwino, ndi chofunikira kuti tichite chiyani tsiku ndi tsiku?
8. Yesu akuitana omtsatira Iye kukhala asodzi a chiyani?
9. Kodi Yesu anali kuchita chiyani m’bwato nthawi ya mphepo yoopsya ya namondwe?
10. Ndi chifukwa chiyani ophunzira ake a Yesu anali kuopa?
11. Yesu anadzudzula ophunzira ake chifukwa sanamkhulupirire Iye ndipo anchita chiyani?
12. Buku Lopatulika liphunzitsa kuti tikakhala m’chitetezo chake sitiyenera kuchita chiyani?

Atangowoloka nyanja ya Galileya m’mphepo yoopsya ya namondwe, Yesu ndi ophunzira ake anafika pa tsidya lina la nyanja ndipo ku malo komweko anakomana ndi amuna awiri amene anagwidwa ndi ziwanda. Anthu amenewo anali oopsya ndipo anakhala ku manda. Mwadzidzidzi mmodzi wa iwo analira kwa Yesu nati, “Kodi tili nanu chiyani, inu Mwana wa Mulungu? Mwabwera kuno kodi kutizunza ife nthawi yake isanafike?”

Pamtunda pa iwo panali gulu lalikulu la nkhumba. Ziwandazo zinapempha Yesu kuti, “Mukatitulutsa, bwanji mutitume ife kuti tikalowe m’gulu la nkhumbalo.” Yesu anziuza ziwandazo kuti, “Chabwino, pitani!” Nthawi yomweyo ziwanda zinatulutsidwa kwa anthuwo nalowa mwa nkhumba. Zitalowedwa ndi ziwanda, nkhumba zinakhala ndi misala. Zinathamangira kunsi kuphompho m’nyanjamo ndipo zinafa m’madzi.

Oweta nkhumbazo anathamanga nawauza onse okhala m’mudzi umenewo nafotokozera zonse zimeneYesu anachita, ndiponso zimene zinachitika ndi anthu ogwidwa ndi ziwanda. Anthu a mudziwo anatuluka kukakumana ndi Yesu napempha Iye kuti achoke kudera kwawo. Yesu anachoka pa bwato nabwerera ku mzinda kwake.

Atangofika ku Galileya anthu anambweretsa munthu wopuwala kwa Yesu. Yesu anam-chiritsa munthu wopuwalayo namkhululukira iye machimo ake. Anthu amene anamuona iye anazizwa nalemekeza Mulungu, koma Afarisi anamganizira Yesu kuti ndi wonyoza Mulungu.

Pambuyo pake posachedwa, Yesu anakomana ndi munthu wokhometsa misonkho ya boma wotchedwa Mateyu. Yesu ananena kwa iye, “Unditsata ine.” Nthawi yomweyo Mateyu anaimirira namtsatira Yesu.

Tsono Yesu ndi otsatira ake anapita masana kunyumba kwa Mateyu kukadya chakudya cha masana. Anthu ambiri okhometsa misonkho ndi anthu ena a mbiri yoipa anadya nawo. Pamene anthu a chipembedzo ndi Afarisi anaona zimenezi anawafunsa otsatira ake a Yesu, “Ndi chifukwa chiyani mphunzitsi wanu akudya ndi okhometsa misonkho ndi ena ochimwa?”

Pakumva zonena zawo, Yesu anawayankha Afarisi, “Iwo amene sadwala safuna sing’anga ayi, koma iwo odwala ndiwo ofuna sing’anga. Koma kamvetsetseni mawu a Mulungu aja akuti, ‘Ndimafuna chifundo, osati nsembe ayi.’”

Tsopano Yesu anachoka pa malo pamenepo nafikira ku anthu a mitundu yonse. Munthu wina amene anali wolamulira anthu ake. Iye anali ndi mtsikana amene anamwalira. Yesu anapita ku mwambo wa maliro, nagwira mtsikanayo dzanja namuutsa iye kwa akufa.

Anapenyetsa anthu awiri akhungu amene anamtsatira namupempha Iye kuti awachiritse. Anabwezeranso munthu wina amene anali wosalankhula koma wogwidwa ndi mzimu woipa. Anatulutsa ziwanda ndipo munthu uja anachiritsidwa.

Yesu anaona zosowa zambiri za anthu, ndipo anamva chifundo. Zosowa zinali zazikulu; anthu anali ngati nkhosa zopanda mbusa. Iye ananena kwa ophunzira ake, “Zokolola zili zochuluka, koma ogwira ntchito ndi ochepa. Pempherani kuti mbuye mwini zokolola atumize antchito ku zokolola zake.”

Tsono Yesu anatenga ophunzira ake nawatumiza iwo ku dera lonse la dziko la Israeli. Anawapatsa iwo mphamvu yokwaniritsa zosowa zambiri za anthu. Cholinga chawo chinali kugawana nawo ndi kuonetsera chikondi cha Mulungu. Anawatumiza ophunzira ake nawalangiza kuti apeze anthu amene adzamvetsera Uthenga Wabwino wa Khristu. Anawauza kuti popeza anthuwo ayenera kukawasiyira mtendere wa Mulungu pa nyumba pawo. Koma Yesu anawachenjeza kuti ambiri adzakana iwo ndi kusamvera mawu awo.

Yesu ananena nawo, “Ndikukutumizani kupita ku nkhosa zimene zili pakati pa mimbulu. Choncho khalani ochenjeza ngati njoka ndi ofatsa ngati njiwa.” Anawauza kuti asadere nkhawa ndi zosowa za thupi. Popeza Mulungu Atate amadziwa ngakhale kuchuluka kwa tsitsi la mutu wathu, ndipo Iye amayang’anira zinthu zonse, natilemekeza ife kwakulu.

Yesu anatsiriza mawu ake asanawatumize iwo kupita nanena, “Amene aliyense adzamwetsa mmodzi wa ang’ono awa chikho chokha cha madzi ozizira, pa dzina la wophunzira, indetu ndinena kwa inu, iye sadzataya mphoto yake.”

MAFUNSO

1. Yesu ndi ophunzira ake atawoloka kutsidya lina la nyanja pakutha pa namondwe, kodi iwo anakomana ndi aydani ?
2. Kodi chinavuta ndi chiyani kwa anthu awiri aja?
3. Yesu anawachitira iwo chiyani?
4. Ndi chifukwa chiyani nkhumba zinadziponya zokha m’nyanja?
5. Ndi chifukwa chiyani anthu a mzinda anapempha Yesu kuti achoke ku dera lawolo?
6. Kodi Yesu anamchitira chiyani munthu wopuwala?
7. Ndi chifukwa chiyani Afarisi anamtchula Yesu kuti ndiye wotukwana Mulungu?
8. Kodi munthu wokhometsa misonkho ya boma amene Yesu anaitana kumtsatira Iye anali dzina lake ndani?
9. Ndi chifukwa chiyani Afarisi anadzudzula Yesu ndi anthu amene anadya limodzi nawo pa malo pamenepo?
10. Kodi Yesu anawayankha Afarisi motani?
11. Kodi Yesu anachita chiyani ndi mwana wodwala wa munthu wolamulira anthu ake?
12. Kodi Yesu anachita chiyani ndi anthu akhungu?
13. Kodi Yesu anachiritsa bwanji munthu amene anali wosalankhula?
14. Kodi Yesu anatumiza ophunzira ake kuchita chiyani?
15. Yesu anauza ophunzira ake kukhala ochenjera ngati chiyani? Anawauzanso kuti akhale ofatsa ngati chiyani?
16. Yesu anawauza kuti asadandaule iwo ndi zinthu za mtundu wanji?
17. Iye ananena kuti Mulungu amadziwa chiyani cha tsitsi lathu?
18. Yesu anawauza ophunzira ake kuti ngati munthu angathe kupereka chikho cha madzi ozizira kwa munthu m’gulu lina la anthu, yemweyo sadzataya mphoto yake. Kodi Yesu analankhula za gulu liti la anthu?

ZOONA ZA UZIMU

1. Yesu amasamalira munthu aliyense. Iye amasamalira anthu ogwidwa ndi ziwanda, odwala, osauka, a chuma, koma makamaka amasamalira ana. Aliyense ndi wofunika ndi wopambana mu Ufumu wa Mulungu.

2. Anthu sasamalira anthu anzawo nthawi zonse. Mu nkhani ya anthu awiri ogwidwa ndi ziwanda, anthu a mzinda wawo anakhumudwa chifukwa cha nkhumba namuuza Yesu kuti atuluke m'dera lawo. Sanasangalale chifukwa choti Yesu anathandiza anthu ena. Iwo anadandaula chifukwa cha kuonongeka kwa chuma chawo. Ndi chinthu chophweka kupeza kufunikira kwake kwa ndalama koposera anthu, koma ambiri a ife tagwa mu msampha umenewo. Mu 1 Timoteo 6:10 tiwerenga kuti, "Pakuti muzu wa zoipa zonse ndiwo chikondi cha pa ndalama; chimene ena pachikhumba, anasochera, nataya chikhulupiriro, nadzipyoza ndi zowawa zambiri." Ndipo mu Mateyu 6:19-21 tiwerenga mawu ake a Yesu akuti, "Musadzikundikire nokha chuma pa dziko lapansi, pamene njenjete ndi dzimbiri zikononga; ndi pamene mbala ziboola ndi kuba: koma mudzikundikire nokha chuma m'Mwamba, pa mene njenjete ndi dzimbiri sizikononga, ndipo mbala siziboola ndi kuba; pakuti kumene kuli chuma chako, komwe kudzakhala mtima wakonso." Ndalama ili ndi mphamvu. Singathe kutilamulira ife…kapena tikhoza kuipereka kwa Ambuye ndipo Iye akhoza kutilamulira.
   *Ganizirani za njira zimene mumaonongera ndalama zanu sabata ndi sabata. Ikhoza kukhala ganizo labwino kulemba njirazi pa kope lanu.
   *Mudzifunse funso ili: Kodi ndimalemekeza Yesu ndi njira zimene ndimaongonera ndalama zanga?
   *Ine kodi ndimagula zinthu kapena kuchita zinthu zimene zimabweretsa ulemu kwa Mulungu? Nanga ndikupweteka anthu ena ndi m'mene ndionongera ndalama zanga? Kodi ndikuthandiza ena ndi m'mene ndionongera ndalama zanga?

M'Chipangano Chakale Mulungu anafuna munthu aliyense kupereka chimodzi cha khumi chimene anali nacho kwa Iye. M'Chipangano Chatsopano, tili kuuzidwa kupereka miyoyo yathu ndi china chilichonse chimene tili nacho kwa Mulungu. Koma m'chikhalidwe chathu, tatsatira za m'Chipangano Chakale lamulo lopereka gawo limodzi la khumi la chuma chathu ku ntchito ya Mulungu kapena ya mpingo. Ichi chimatchedwa "chakhumi." Yambani kupemphera tsopano: Kodi Ambuye akufuna kuti ndipereka ndalama zingati zanga ku ntchito yake? Mawu a Mulungu amaphunzitsa kuti Mulungu amadalitsa iwo amene adzapereka kukuza Ufumu wake. Amaphunzitsanso kuti Yesu adzakwaniritsa zosowa zathu. Mutha kuganizira, "Koma Mulungu sadziwa za umphawi wanga ine!" "Iye sazindikira ngongole zazikulu zimene ine ndili nazo!" Yesu anabadwira m'banja la anthu osauka pa dziko. Iye amazindikira mavuto a umphawi, koma Iye akutipempha ife tonse kuti tikhale okhulupirika ndi omvera pa zinthu zina zili zonse zimene atipempha ife kuti tichite. Pemphani Ambuye m'mene Iye akukufunirani kuti mukhale mbali ya kuthandizira pa kupereka chuma chanu ku utumiki wake.

3. Kukhala otsatira ake a Yesu kutanthauza kuti tikutsatira chitsanzo chake ndi kukonda ena monga momwe Iye amawakonda. Ndi zoona kuti sitingathe kuchiritsa anthu monga anachita Yesu, komabe Yesu amachiritsa anthu. Tiyenera kukhala okhulupirika pa kupempherera odwala. Tiyenera kukhala pafupi nawo ndi kuwagwira dzanja pa nthawi ya vuto. Tiyenera kuwauza za chikondi chake cha Yesu kwa iwo. Tiyenera kuwapempherera ogwidwa ndi ziwanda. Ngakhale mpaka lero Yesu amatulutsabe mizimu yoipa m'malo ambiri pa dziko lapansi kupyolera mu mapemphero a anthu ake. Tiyenera kuwapempherera ndi kuthandiza anthu osauka. Tiyenera kuyesetsa kuthandiza m'mene tingathere pa zosowa za thupi, koma chofunikira ndi kuwauza anthu za chikondi cha Ambuye amene akhoza kusintha miyoyo yawo ya mkati mwa mtima. Makamaka tiyenera kuthandiza ana. Yesu analamulira omtsatira Iye kuti achite zonsezi. Koma Iye analonjeza mphoto yopambana kwa anthu amene adzasamalira ana.

4. Ndi chinthu chovuta kukonda anthu ena, koma Mulungu amafuna kuti tikhale a chifundo. Anthu okhometsa misonkho ya boma mu nthawiyo sanali okondedwa pa zifukwa zabwino. Anagwira ntchito mu boma la ziphuphu kusonkhetsa ndalama kwa anthu, ndipo ena mwa iwo analamula anthu kupereka mochuluka koposera m'mene anayenera, nasunga ndalama yoonjezera m'thumba mwawo. Kusonyeza chikondi kwa munthu wina

amene wakuberani chinthu china kwa iwe si chinthu chophweka kuchichita, makamaka munthuyo akapanda kulapa pa zimene wachitazo. Komabe Yesu atiuza ife kuti monga omtsatira Iye, sitiyenera kuwadzudzula anthu amenewa ngakhale mwina zimene iye akuchita ndi zinthu zosayenera. Udindo wathu ndi kuwapempherera iwo, kuwakonda, ndi kuwaonetsera zoonadi za chikhulupiriro chake cha Mulungu. Ngati alapa machimo awo, iwonso adzatha kulandira chikhululukiro chenicheni cha Mulungu. Mawu a Mulungu anena kuti ife tonse ndi ochimwa ndipo tiyenera kulangidwa. Anenanso kuti tonse talandira chikhululukiro ndi chifundo. Tsono ife tiyenera kuonetsera chikhululukiro ndi chifundo, ngakhale kuti izi ndi zovuta kwa ife kuchita kopanda mphamvu yake ya Mulungu m'miyoyo yathu.

5. Zosowa za anthu a pa dziko lapansi ndi zazikulu kwambiri; ife sitingathe kuchita zimenezi pa tokha. Kuli anthu zikwi zambiri amene sanadziwe za chikondi cha Yesu. Ndiponso kuli anthu zikwi zambiri amene sanadziwe chikondi cha wina aliyense. Kuli anthu zikwi zambiri amene adzapereka miyoyo yawo kwa Yesu ndi kudziwa chikondi chake ngati wina awasonyeza iwo njira ya kumtsatira Iye.

6. <u>Inu mutha kuonetsera chikondi chanu kwa Mulungu ndi kwa wina ndi mnzake pa kupereka chakhumi chanu ku ntchito ya Mulungu kupyolera mu mpingo wanu</u>. Mulungu amagwiritsa ntchito mpingo kutumikira anthu pa zosowa zawo za uzimu, za thupi, ndi za m'mtima.

MAFUNSO OKAMBIRANA

1. Kodi ndi njira ziti zimene ndikhoza kuonetsera chikondi cha Mulungu kwa anthu ena?
2. Kodi zosowa zazikulu kwambiri za anthu ondizungulira ine ndi ziti?
3. Kodi ndikhoza bwanji kuthandiza anthu ovutika amene ali pafupi ndi ine?
4. Kodi ndikhoza bwanji kuonetsera chikondi cha Mulungu kwa ana?
5. Ndi mu njira ziti zimene ndimalola ndalama kukhala chopambana ndi anthu m'moyo mwanga?
6. Kodi ndimalemekeza Mulungu ndi ndalama zanga?
7. Kodi ndikhoza bwanji kuonetsera chifundo cha Mulungu kwa anthu m'moyo mwanga?

*Iyi ndi nthawi yabwino yokambirana dongosolo la kuthandiza wamishoni ku dera lina la dziko ndi kupempherera pfuko la anthu a dziko lina amene sanamve za chikondi cha Mulungu.

Kuyamba Moyo Watsopano mwa Yesu

Nkhani Zoona Zochokera mu Buku la Mateyu

Kuperekedwa ndi Chikhululukiro

Phunziro 6, Mateyu 21-27:10

“Ngati tivomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye kuti atikhlulukire machimo athu, ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama chili chonse.” 1 Yohane 1:9

KUBWEREZA

1. Mneneri Yesaya analosa kuti Yesu adzatchedwa “Imanuele” limene limasulidwe kutanthauza chiyani?
2. Yesu ananena kuti ndi yani yekha amene akudziwa tsiku limene Iye adzabweranso?
3. Yohane anabatiza anthu ambiri amene anadza kwa iye m’chipululu. Kodi iwo analapa chiyani?
4. Yesu anayankha Satana katatu pogwiritsa ntchito chiyani?
5. Ngati timafuna kumudziwa Mulungu bwino, ndi chofunikira kuti tichite chiyani tsiku ndi tsiku?
6. Yesu akuitana omtsatira Iye kukhala asodzi a chiyani?
7. Yesu anaonetsa chikondi chake kwa anthu pa kuchita chiyani ndi nthenda zawo?
8. Yesu anagwidwa nacho chifundo ndi anthu chifukwa cha zinthu zambiri zotani za iwo?
9. Yesu anauza ophunzira ake kukhala ochenjera ngati chiyani? Anawauzanso kuti akhale ofatsa ngati chiyani?
10. Iye ananena kuti Mulungu amadziwa chiyani cha tsitsi lathu?
11. Yesu anawauza ophunzira ake kuti ngati munthu angathe kupereka chikho cha madzi ozizira kwa munthu m’gulu lina la anthu, yemweyo sadzataya mphoto yake. Kodi Yesu analankhula za gulu liti la anthu?
12. Pamene anali m’bwato pakati pa mphepo yayikulu, Yesu anawauza ophunizra ake kuti sayenera kuchita chiyani ?

Yesu anaphunzitsa, kulalikira, ndi kuchiritsa anthu ambiri m’dera la Galileya, koma ena ambiri anakana mawu ake. Yesu anafotokozera ophunzira ake kuti izi zinali m’dongosolo lake la Mulungu kuti anasankha kuwabisira choonadi chake kwa anzeru ndi ochenjera ndipo kuukira izo kwa makanda.

Nthawi inafika imene anachenjeza otsatira ake kale. Inali nthawi yake yopita ku Yerusalemu kuti akavutitsidwa ndi akulu a ansembe ndi ena a chipembedzo kuti aphedwe ndi kuti akautsidwa kwa akufa.

Kubwera kwake ku Yerusalemu kunali kopambana. Anthu anaima m’mphepete mwa msewu ku mbali wake wonse nayala zovala zawo pa njira, ndipo ena anadula nthambi za kanjedza naziyala m’njiramo. Pamene anapita pakati pawo anali kukwera pa bulu. Khamu lomtsogolera ndi lomtsatira Iye linafuula kuti, “Hosana kwa Mwana wa Davide! Wolemeke-zeka ndiye wakudza m’dzina la Ambuye! Hosana kumwambamwamba!”

Yesu anakhala masiku angapo ku Yerusalemu kuphunzitsa m’nyumba zopemphereramo za Ayuda, kulalikira ndi kuchiritsa anthu ambiri. Koma kunalinso ambiri a Afarisi ndi Asaduki amene anatsutsana ndi kumvutitsa Iye.

Yudasi Iskariote, mmodzi mwa ophunzira ake a Yesu, anapita kwa akulu a ansembe nawafunsa kuti, “Kodi mudzandichitiranji ndikadzampereka Yesu kwa inu? Iwo anampatsa ndalama za siliva makumi atatu.

Pa usiku wa chikondwerero cha Paska, tsiku lopambana la utchuti wa Ayuda m’chaka chawo, Yesu ndi ophunzira ake anakhala pamodzi nkumadya. Ndipo pokudya iwo, Yesu anatenga mkate naunyema nati, “Tengani, idyani, ichi ndi thupi langa.” Kenaka anatenga chikho cha vinyo nathokoza Mulungu, nanena, “Imwani ichi inu nonse, pakuti ichi ndi mwazi wanga wa chipangano chatsopano, umene wakhetsedwa kwa anthu ambiri pa kukhululukira machimo awo.”

Pambuyo pa chakudya, onsewo anapita ku phiri la Azitona. Kumeneko Yesu anawachenjeza ophunzira ake kuti iwo onse adzakhumudwa. Petro ananenetsa kuti ngakhale onse adzakhumudwa chifukwa cha Yesu, iye yemwe sadzamsiya. Yesu analosera kuti sikuti adzangomsiya Iye, koma kuti adzamkana Iye katatu tambala asanalire usiku womweo.

Kuchokera kumeneko, Yesu anatenga ophunzira ake napita nawo ku Getsemani. Anakhala nawo usiku wonse kupemphera. Iye anamva chisoni chachikulu ngakhale chomtengera Iye ku imfa chifukwa cha zimene zinali kumuonekera. Anapempha ophunzira ake kuti apemphere naye limodzi. Koma onse anagona tulo, kunali mpaka kufika kwake kwa Yudasi kuti anauka. Yudasi anabwera pamodzi ndi ansembe ndi anthu ena kudzamgwira Yesu.

Yudasi anafika kwa Yesu nampsyopsyona ngati chizindikiro chompereka Iye. Akulu a ansembe anamgwira Yesu namtengera ku nyumba ya Kayafa, mkulu wa ansembe onse nthawi imeneyo. Ophunzira ake a Yesu anathawa ku Getsemani.

Pamene Yesu anali m'nyumba kukazengedwa mlandu ndi Kayafa ndi atsogoleri ena, Petro anali kunja kwa mpanda. Pokhala iye apo, mkazi wina anafika kwa iye nanena, "Iwenso unali ndi Yesu wa ku Galileya." Koma Petro anakana, ndipo anasunthira pa chipata nayembekezerapo kufikira mtsikana winanso anamuona namunena kuti iye anali ndi Yesu. Petro anakananso nthawi imeneyi analumbira. Posachedwa anthu ena anampeza Petro nanena kuti anali ndi Yesu. Nthawi imeneyi anayamba kutemberera ndi kulumbira nanena, "Ine sindimdziwa konse!" Nthawi yomweyo tambala analira, ndipo Petro anakumbukira mawu a Yesu, ndipo anachoka nakalira kwakukulu.

Nthawi ya ku m'mawa, akulu ansembe anamtenga Yesu kwa Pilato kuti akaphedwe. Yudasi atamva ndi kuona kuti Yesu anaweruzidwa chilango cha imfa anamvadi chisoni ndipo anafuna kukabwezera ndalama zija kwa akulu ansembe. Ananena kwa Iwo, "Ndachimwa chifukwa cha kupereka munthu wosalakwa." Iwo anamuyankha iye, "Ichi ndi chiyani kwa ife? Uona wekha za izo!" Yudasi anaponya ndalama zija pansi m'kachisi nachoka napita kukadzikhweza yekha pa mtengo.

MAFUNSO

1. Ndi dongosolo la Mulungu kubisira choonadi chake kwa anzeru ndi ochenjeza ndi kuululira kwa ayani?
2. Kodi Yesu anachitidwa motani pamene analowa mu mzinda wa Yerusalemu?
3. Ndi chifukwa chiyani Yudasi anadza kwa akulu ansembe? Nanga chifukwa chiyani iwo anampereka ndalama za siliva makumi atatu?
4. Pakati pa chakudya chake chotsiriza cha Paska pamodzi ndi ophunzira ake, Yesu anawauza kuti vinyo amene anamwa ndi mkate umene anadya anali apadera. Nanga ndi chifukwa chiyani?
5. Ndi chifukwa chiyani Yesu anawauza ophunzira ake kuti mwazi wake uyenera kukhetsedwa?
6. Pa phiri la Azitona Yesu anauza omtsatira ake kuti adzakhumudwa. Petro anakana zimenezi. Kodi Yesu analosera chiyani za Petro?
7. Kodi Yudasi anapereka Yesu ndi chizindikiro chotani?
8. Kodi Petro anali kuti pamene akulu ansembe anali kuweruza Yesu?
9. Atsikana awiri anabwera nthawi zosiyana kwa Petro namnenera zinthu zina kwa iye. Kodi anamnenera iye chiyani?
10. Pa nthawi yokwanira katatu anthu ena anabwera kwa Petro nanenanso kuti iye anali ndi Yesu. Nanga Petro anawayanka bwanji?
11. Kodi inali nthawi yiti imene Yudasi anamvadi chisoni chifukwa choti anapereka Yesu?
12. Ndi chifukwa chiyani Yudasi anabwereranso kwa akulu ansembe?
13. Kodi Yudasi anachita chiyani akulu ansembe atakana kulandira ndalama zoperekera Yesu?

ZOONA ZA UZIMU

1. Yesu pokudya potsiriza ndi ophunzira ake, Iye anayamba mwambo umene watsatidwa ndi omtsatira ake onse pa dziko lonse lapansi kufikira lero. Timatchula mwambo uwu "Mgonero wa Ambuye." Mgonero wa Ambuyu si chinthu chodabwitsa chimene chikuchotsa machimo athu kapena kuchita chinthu china chachilendo pa matupi athu. Si nthawi imene mkate ndi vinyo amasanduka matsenga kukhala thupi ndi magazi a Yesu enieni. Koma ndi nthawi ya kuti otsatira ake akhala limodzi, kudya mkate ndi kumwera chikho ndi kukumbukira nsembe imene Yesu anapereka pa mtanda. Ndi nthawi yokumbukira dipo limene Yesu analipira ya machimo athu. Ndi nthawi ya chimwemwe ndi kuyamkia tikakondwerera limodzi chifukwa cha chikhululukiro chimene Iye anatigulira ife. Mawu a Mulungu amaphunzitsa mu 1 Akorinto 11:23-33 kuti mgonero ndi nthawi imene tiyenera kukhala chete, si nthawi yochita mopepusa. Ndi nthawi yoganizira nsembe imene Iye anatiperekera ife ndi kuyesa mitima yathu chifukwa cha zimene Iye watichitira ife pa mtanda.

2. Mulungu anadziwa zolakwa zathu ngakhale tisanamdziwe Iye, ndipo Iye amativomerezabe ife ndipo amafuna kutigwiritsa ntchito ife mu Ufumu wake. Kuchokera ku nthawi imene Yesu anaitana Petro kukhala "msodzi wa anthu," anadziwa kuti usiku womwewo Petro adzamkana Iye. Koma tiwerengenso m'buku la Machitidwe a Atumwi kuti Mulungu anagwiritsa ntchito Petro kubweretsa anthu zikwi zambiri kwa Yesu. Ngakhale m'Mawu a Mulungu muli mabuku awiri olembedwa ndi Petro. M'mutu wachiwiri wa buku la Machitidwe a Atumwi tikhoza kuwerenga za nthawi imene Yesu anabwerera kumwamba, tipeza Petro ali kulalikira uthenga ku Yerusalemu kwa anthu amene ankawachitira mantha pa usiku umene Yesu anaperekedwa.

   Momwemonso, zolakwa zathu sizikhala zachilendo kwa Mulungu. Ngakhale titavomereza Yesu tidzakhala ndi zolakwa zina m'miyoyo yathu. Ndithu tidzachimwa, tidzampereka Iye, ndipo tidzachita zomwezo zimene timazidana.

3. Tsono nanga tichite chiyani tikalakwa pamaso pa Mulungu?

   Kunali anthu awiri amene anapereka Yesu kwa adani ake usiku uwenewo. Munthu wina anali Petro, amene anapereka Yesu, koma patsogolo pake anagwiritsidwa ntchito ndi Mulungu kwakukulu. Wina anali Yudasi, amene anaperekanso Yesu, koma iye anadzikhweza yekha pa mtengo. Anthu ambiri amalakwitsa poganiza kuti Petro anadzakhoza ndi kuti Yudasi analephera chifukwa cha kumpereka kwake kunali kwakulu koposa. Izi si choncho ayi. Mawu a Mulungu amaphunzitsa kuti TONSE tili ochimwa. Ife tonse timapereka Mulungu ndi kuthawa chilango cha muyaya chifukwa cha kumpereka Iye. Koma ngati izi si zoona, kodi nanga cholakwa cha Yudasi chinali chiyani? Ndi kuti Yudasi sanalape machimo ake nafuna chikhululukiro cha Mulungu.

Alipo anthu ambiri amene amadziwa kuti achimwa. Ambiri amayesa kuti ndi kovutadi kukhala wolakwa ndi kuzindikira zimene achita zosayenera pa moyo wawo. Anthu ena achita zoopsya zazikulu zimene amaganizira kuti Mulungu sangathe kuwakhululukira zinthu zimenezi. Koma Mawu a Mulungu amaphunzitsa kuti IZI SI ZOONA.

1 Yohane 1:9 likuti, "Ngati tivomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye kuti atikhlulukire machimo athu, ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama chili chonse." Izi zitanthauza kuti munthu akabwera kwa Mulungu, namuuza Mulungu chimene wachita, nalapa, napempha Mulungu kumkhululukira machimo ake, Mulungu ali wokhulupirika kumkhululukira iye tchimo lina lilichonse ngakhale ndi loopsya kwambiri. Nsembe imene Yesu anadzipereka yekha pamene anali pa mtanda ndi yopambana kokwaniritsa tchimolo.

Komanso zitanthauza kuti monga omtsatira Yesu, sitiyenera kumakhala m'moyo wogonjetsedwa m'machimo. Tiyenera kukumbukira kuti machimo athu a kale akhululukidwe ndi Mulungu. Sitiyenera kukhala otsutsidwa ndi machimo amene Yesu anakhululukira kale. Petro analapa machimo ake ndipo Mulungu anamgwiritsa ntchito iye. Ifenso tiyenera kulapa machimo athu kuti Mulungu atigwiritsa ntchito ife.

Kwenikweni Yudasi anali ndi zoipa mu mtima mwake. Chinali chinthu chovuta kupereka bwenzi la pamtima, ndi kupangitsa munthuyo kuvutitsidwa pa imfa ngakhale kuti iye anali wopanda chifukwa china chilichonse. Mulungu anali ndi chikonzero pa moyo wake wa Yudasi. Komabe Mulungu anakhalabe ndi cholinga ndi moyo wake wa Yudasi. Ngakhale Yudasi akadakhululukidwa ndi Mulungu akadangobwera kwa Yesu. Koma analola cholakwacho kulamulira moyo wake ndipo matsirizo ake anatenga moyo wake.

4. Yesu anawauza ophunzira ake kuti chipangano chathu kapena chigwirizano chathu ndi Mulungu chimatheka chifukwa cha mwazi wa Yesu umene unakhetsedwa pokhululukira Machimo athu. Ife sitinachite china chilichonse kuti tilandire chikhululukiro cha machimo m'miyoyo yathu. Pambuyo pakuvomereza Yesu m'mtima palibe china tingachite kuti tiluze chikhululukirochi. Mu Aefeso 1:13,14 tiwerenga kuti, "…ndi kumkhulupirira Iye munasindikizidwa chizindikiro ndi Mzimu Woyera wa lonjezano, ndiye chikole cha cholowa chathu, kuti ake ake akaomboledwe, ndi kuti ulemerero wake uyamikike." Yohane 3:16 ikuti muli ndi "woyo wosatha." Pambuyo pa Yesu kulowa m'moyo mwanu samakusiyani inu. Mwapulumutsidwa kwa muyaya kuchokera pa nthawiyo mpaka patsogolo. Buku Lopatulika linena kuti tiyenera kukumbukira nsembe imene Yesu anapereka kwa ife kuthetsa kuti tisachimwe. Tiyenera kuchita m'mene tingathe kuti tikhale tsiku ndi tsiku pa moyo wathu kumvera Iye. 1 Yohane 2:1 imatikumbutsa kuti tikachimwa tiyenera kukumbukira Iye amene ali mkati mwa ife. Tiyenera kukumbuka kuti Yesu ali m'miyoyo yathu ndi kuti ndiye nkhoswe yathu pamaso pa Mulungu. Iye ndi wolowa m'malo mwathu kulipira machimo athu.

MAFUNSO OKAMBIRANA

1. Kodi mukuganiza bwanji za Petro ndi Yudasi?
2. Kodi liwu lakuti, "kukhululukidwa" litanthauzanji kwa inu?
3. Kodi mwakhalapo wolola kuti mukhoza kufanana ndi Yudasi?
4. Musanene china chake mokweza, koma kodi ndi kotheka kuti mwachitapo china choopsya chimene mwaona kuti ndi vuto lakuti muvomereze Yesu kukhululukira moyo wanu?
5. Kodi mawu a Yesu anena chiyani kwa inu mu nthawiyi?
   Wina aliyense atchule ndime ya pamtima kapena aiwerenge pa 1 Yohane 1:9.

Munthu aliyense ayenera kugwetsa mutu wake pansi ndi kulankhula ndi Mulungu za zonse zimene zili m'mtima mwake. Ngati pali tchimo, livomerezeni. Pemphani Mulungu kuti akuchotsereni kutsutsa kwake kwa tchimoli. Pemphani Mulungu, pa chifundo chake kuti akuikeni patali pa tchimoli. Vomerezani poyera kuti nsembe yake ya Yesu pa mtanda ndi yokwanira kukhululukira machimo anu. Vomerezani choonadi ichi.

*Zitheka mwina mwake patsogolo kuti Satana adakutsutsani inu ndi maganizo a zolakwa zanu. Maganizo amenewa sachokera kwa Mulungu ayi! Satana amafuna kuti mutstutsidwe ndi maganizo a bodza lake. Mukayamba kutsutsidwa ndi maganizowa, za zoipa zimene Mulungu akukhululukirani kale, imani posakhalitsa ndi popempherani:

> "Zikomo Yesu chifukwa cha chikhululukiro cha tchimo langa (nenani tchimolo). Ambuye ndikuthokozani chifukwa nsembe yanu ndi yopambana kundikhululukira ine. Ndikhulupirira kuti mwazi wanu wandiyeretsa ku tchimoli, ndipo ndikupemphani kuti mundichotsere maganizowa amene amanditsutsa."

Mulungu ndi wokhulupirika ndipo adzachita zimenezi. Ngati mupemphera kwa Mulungu nthawi iliyonse imene Satana akutsutsani, posachedwa adzasiya. Ndipo mudzakhala mfulu wa izi za m'maganizo mwanu. Tili ndi chigonjetso chokwanira ku mbali iliyonse ya moyo wathu mwa Yesu!

Kuyamba Moyo Watsopano mwa Yesu
Nkhani Zoona Zochokera mu Buku la Mateyu
Kupachikidwa Kwake Kwa Yesu
Phunziro 7, Mateyu 26-27

"Pakuti mawu a mtanda ali ndithu chinthu chopusa kwa iwo akutayika, koma kwa ife amene tili kupulumutsidwa ali mphamvu ya Mulungu." 1 Akorinto 1:18

KUBWEREZA

1. Mneneri Yesaya analosa kuti Yesu adzatchedwa "Imanuele" limene limasulidwe kutanthauza chiyani?
2. Yesu ananena kuti ndi yani yekha amene akudziwa tsiku limene Iye adzabweranso?
3. Yohane anabatiza anthu ambiri amene anadza kwa iye m'chipululu. Kodi iwo analapa chiyani?
4. Yesu anayankha Satana katatu pogwiritsa ntchito chiyani?
5. Ngati timafuna kumudziwa Mulungu bwino, ndi chofunikira kuti tichite chiyani naye tsiku ndi tsiku?
6. Yesu akuitana omtsatira Iye kukhala asodzi a chiyani?
7. Yesu anawauza ophunzira ake kuti pakuti ali pakati pawo, iwo sayenera kuchita chiyani?
8. Yesu anatha nthawi yake pa dziko pa kuchita chiyani m'nyumba zopemphereramo? Kodi analalika Uthenga Wabwino wonena za Ufumu wuti? Kodi anachita chiyani ndi nthenda za anthu?
9. Yesu anauza ophunzira ake kukhala ochenjera ngati chiyani? Anawauzanso kuti akhale ofatsa ngati chiyani?
10. Iye ananena kuti Mulungu amadziwa chiyani cha tsitsi lathu?
11. Pa phiri la Azitona Yesu analosera kuti mmodzi mwa ophunzira ake adzampereka Iye tambala asanalire. Kodi wophunzira ameneyo anali yani?
12. Wophunzira wake wa Yesu amene anampereka Iye ndi ndalama za siliva makumi atatu anali yani?
13. Anali wophunzira wuti amene analapa kuti anapereka Yesu ndi pambuyo pake anagwiritsidwa ntchito kwakukulu ndi Mulungu?
14. Anali wophunzira wuti wa Yesu amene antsutsidwa m'mtima chifukwa anapereka Yesu ndi pambuyo pake anadzikhweza yekha pa mtengo?
15. Buku Lopatulika litiphunzitsa kuti tiyenera kuchita chiyani ndi machimo athu? Ndipo titatero, nanga Mulungu atichitira ife chiyani ndi machimo athu? Nanga atichitira ife chiyani ndi chosalungama chathu?

Pamene Petro anali kunja kwa khomo la Kayafa, Yesu anali mkati mozengedwa milandu yambiri yonamizira Iye. Mwa milandu yonse sanathe kupeza ngakhale umodzi wotsutsa Iye. Yesu analola omzenga Iye mlandu kupitiriza kumpeza Iye wolakwa ngakhale sanatsegule pa kamwa pake kuti adziteteze. Atalephera kukwaniritsa chilichonse, Kayafa anafunsa Yesu, "Utiuze ngati iwe ndiwe Khristu, Mwana wa Mulungu!"

Potsiriza, Yesu anawayankha poti, "Mwatero, koma ndinenanso kwa inu, Kuyambira tsopano mudzaona Mwana wa munthu ali kukhala ku dzanja lamanja la mphamvu, ndi kufika pa mitambo ya kumwamba."

Ichi chinali chitsimikizo chokwanira cha Kayafa, ndipo anakhuza chovala chake nanena kuti Yesu ndi wamwano. Anatenga Yesu, namlavulira Iye pa nkhope pake, namlalitira Iye, ndipo ena anamuwomba Iye makofi.

M'mawa wa tsiku linalo ansembe ndi atsogoleri a chipembedzo anamtenga Yesu kupita naye kwa mkulu wa Chiroma woyang'anira dera la Yudeya, dzina lake Pilato. Anamfotoko-zera Pilato kuti Yesu anadzitchula iyeyo ali mfumu ya Ayuda. Pilato anamtenga ndi kumfunsa Iye funso, "Kodi iwe ndiwe mfumu ya Ayuda?" Yankho lake linali lalifupi, "Pakuti inu mwatero." Kenaka akulu a ansembe analankhula ndandanda zawo zotsutsa Iye, komabe Yesu sanayankhe. Pilato anadabwa chifukwa cha kukhala chete kwa Yesu posayankhapo kanthu. Sanathe kupeza cholakwa pa Yesu ndipo anayesa kupeza njira ya mtendere ya kumumasulira Yesu.

Chaka chilichonse mu nthawi ya Paska inali njira yake ya chizolowezi cha Pilato kuti atulutse mmodzi wa m'ndende amene anthu angasankhe. M'chaka chimenecho munali wa m'ndende woipititsa, dzina lake Barabasi. Tsono Pilato anabweretsa Barabasi ndi Yesu napereka mpata khamu nati, "Kodi mukufuna tikumasulereni yani, Barabasi kapena Yesu otchedwa Khristu?" Koma anthu ovundulika ndi Afarisi anakuwa limodzi, "Barabasi!" Pilato anatembenukira kwa anthu, "Chifukwa chiyani? Tchimo lake wachita ndi lotani?" Yankho lawo linali, "Lolani apachikidwe!" Tsono Pilato, ataona kuti anthu anayamba chipolowe, anatenga madzi nasamba manja ake nati, "Ine ndilibe kuchimwira mwazi wa munthu wolungama, mudzionere nokha." Pomwepo anawamasulira iwo Barabasi, koma analamulira kuti Yesu akwapulidwe ndi kumtumiza ku likulu kumene adzapitiriza kulandira mazunzo ena.

Kumeneko asirikali anavula malaya ake namveka Iye ndi malaya ofira achifumu. Ndipo analuka chisoti cha minga nachiika pa mutu pake, namgwiritsa ndodo m'dzanja lamanja lake; ndipo anagwada pansi pamaso pake nasewera naye mwa chipongwe nati, "Tikuoneni, Mfumu ya Ayuda!" Anamthira malovu natenga ndodo nampanda Iye pa mutu. Atatha kusewera naye anavula malaya aja namveka Iye malaya ake napita naye ku malo otchedwa Gologota kapena "Malo a Chibade cha Mutu" kuti akampachike pa mtanda. Pa njira asirikali analamulira munthu wotchedwa Simoni kuti anyamule mtanda wake wa Yesu.

Pamene Yesu anali chipachikidwire pa mtanda, asirikali anagawana zovala zake nachita maele kuti aone zidzakhala za yani. Iwo anamuona Iye ali kufa pa mtanda. Akulu a ansembe ndi akulu ena anabwera kumuona Iye atapachikidwa, anamuseka Iye napereka mawu onyoza kuti bwanji sangathe kudzipulumutsa yekha pa mtandapo. Anthu ena ambiri anabwera ku malo amene anapachikidwa napukusa mitu yawo kupereka umboni wa chipongwe. Ngakhale mbala ziwiri zinapachikidwa pafupi ndi Iye mbali zonse za dzanja lake. Ndipo zomwezo anamnenera Iye mawu owawitsa.

Nthawi itangokwana ola lachisanu ndi chimodzi kukafika pa ola lachisanu ndi chinayi pamene Yesu anali chipachikiridwe pa mtanda, mdima waukulu unakuta pa dera lonse pa-dziko. Itangokwana ola lachisanu ndi chinayi Yesu analira nafuula, "Eli, Eli, lamasabakatani?" Kutanthauza kuti "Mulungu wanga, Mulungu wanga, mwandisiyiranji ine?" Patangotha nthawi yochepa analira kachiwiri nafuula ndi mawu akulu napereka mzimu wake.

Nthawi imene atangopereka mzimu wake, zinthu zambiri zozizwitsa zinachitika. Chinsalu cha m'kachisi chinang'ambika pakati kuchokera kumwamba kufikira pansi. Dziko linagwede-zeka, ndi miyala yambiri inang'ambika. Manda ambiri anatseguka, ndipo anatuluka anthu ambiri a Mulungu amene anamwalira kale, anauka kwa akufa. Anatuluka m'manda, ndipo Yesu, atauka kwa akufa, iwo analowa m'Yerusalemu naonekera ndi anthu ambiri.

Madzulo pa imfa yake ya Yesu, munthu wina wachuma wa ku Arimateya dzina lake Yosefe anapita kwa Pilato nakapempha thupi la Yesu kuti akaliike m'manda. Pilato anavomereza, ndi Yesu thupi lake analitenga nakaliika m'manda mwatsopano m'mene anasemedwa ndi mwala. Yosefe anatenga thupi la Yesu nakulunga thupilo ndi nsalu ya bafuta, namuika Yesu mkati mwa manda natsekera pa khomo ndi chimwala chachikulu polowera manda. Pambuyo anachoka ndi Maria wa Magadala ndi Maria wina pa malopo.

MAFUNSO

1. Atsogoleri a Ayuda potsiriza anamweruza bwanji Yesu kwa Kayafa?
2. Yesu anawayankha bwanji zonse zimene iwo anali kumlankhulira Iye?
3. Pilato anaonetsera chiyani ataona kuti Yesu sanayankhe kena kalikonse kwa iwo omzenga Iye milandu?
4. Kodi Barabasi anali yani?
5. Asirikali a Chiroma anamuchita chiyani Yesu?
6. Kodi ansembe ndi ena openyera anamuchita chiyani Yesu pokhala Iye pa mtanda?
7. Chinachitika chiyani pa dziko lonse lapansi pakati pa ola lakhumi ndi chiwiri ndi ola lachitatu?
8. Kodi Yesu analira chiyani asanapereke mzimu wake kwa Mulungu?
9. Zinthu zachilendo ziti zinachitika pa kufa kwake kwa Yesu?
10. Kodi Yosefe wa ku Arimateya anachita chiyani ndi thupi la Yesu?

ZOONA ZA UZIMU

Zochita za Mulungu si zochita za munthu. Tiyeni tiwerenge limodzi ndime za 1 Akorinto 1:18-21,27. Werengani ndimezi kawiri kapena katatu, choncho aliyense akhale ndi nthawi yoganizira zimene Mawu a Mulungu akunena.

"Pakuti mawu a mtanda ali ndithu chinthu chopusa kwa iwo akutayika, koma kwa ife amene tili kupulumutsidwa ali mphamvu ya Mulungu. Pakuti kulembedwa:

> 'Ndidzaononga nzeru za anzeru, ndi kuchenjera kwa ochenjera ndidzakutha.'

Ali kuti wanzeru? Mlembi ali kuti? Ali kuti wotsutsana wa nthawi ya pansi pano? Kodi Mulungu sanaipusitsa nzeru ya dziko lapansi? Pakuti popeza m'nzeru ya Mulungu dziko lapansi, mwa nzeru yake, silinadziwa Mulungu, chinamkonda Mulungu kupulumutsa okhulupirawo choposa cha kulalikira…koma Mulungu anasankhula zopusa za dziko lapansi kuti akachititse manyazi anzeru; ndipo zofooka za dziko lapansi Mulungu anazisankhula kuti akachititse manyazi zamphamvu."

Poona m'moyo wa Yesu Khristu, tiona kuti zochita za Mulungu si zochita za munthu.

*Mfumu yadziko ikabadwa, iyo imabadwira m'nyumba ya chifumu. Koma Mulungu anatumiza Yesu, Mfumu ya Mafumu, kuti akabadwe mu umphawi.

*Munthu wina akamalengeza uthenga wofunikira kapena kubwera kwa munthu wofunikira, wotumiza uthengayo amakhala wachuma, wovala zovala bwino ndipo amayenda pa galimoto yabwino. Mulungu anatumiza Yohane Mbatizi wovala zovala za ubweya wa ngamila kukalengeza m'chipululu za kubwera kwa Yesu, kumene anthu anapita kukamvera za uthenga umenewo.

*Mfumu ya dziko ikakhala ndi mdani mmene iye ali oposera mphamvu, amugonjetsa mofulumira. Yesu anapita dala m'chipululu kukayesedwa ndi Satana, koma sanamu-ononge iye, ngakhake kufikira tsopano.

*Mfumu ya dziko ikamasankha anthu anzake, imasankha anthu amene aphunzira sukulu zapamwamba, ochokera mabanja abwino, ndi amene ali a chuma. Yesu anasankha ena mwa anthu a pansi, asodzi ndi okhometsa misonkho.

*Mfumu ya dziko imaumiriza anthu awo kuti azimvera iye, ndipo ikupereka chilango kwa iwo onyoza iye. Yesu anatiphunzitsa ife kukonda. Iye amalola anthu kusankha kumtsatira Iye kapena kumkana Iye.

*Mfumu ya dziko imalemba anthu ena omugwirira ntchito, kulipira msonkho, ngakhale kupha ena ofuna kuukira boma lake. Yesu anafera pa mtanda mwadala chifukwa anafuna kulipira dipo la machimo athu. Iye akufuna kuti tikhale afulu kukhala muyaya ndi Iye.

*Mfumu ya dziko ikafa, iyo imaikidwa, ndipo mwana wake amalowa m'malo mwake. Yesu atafa, anaukanso ndi kuchitira ufumu kwa muyaya.

Yesu sali ngati munthu. Iye ndi Mulungu. Iye ayenera kupembedzedwa, kukondedwa, ndi kumveredwa. Amatikonda ife, ndipo atifunira ife zabwino. Moyo wake pa dziko lino ndi wopambana ndi wosazindikirika. Zochita zake za Mulungu zili zazikulu koposa kuti tisangazizindikire.

* Mawu a Mulungu amaphunzitsa kuti Ambuye amakonda kumva matamando a anthu ake. Kutama kumatanthauza kumuuza Yesu kuti mukumkonda Iye ndi kuti mukumsimba Iye chifukwa cha zinthu zonse zopambana zimene Iye ali nazo. Mulungu amakonda kumva anthu ake kunena mawu monga awa: "Ndikuyamikani Ambuye chifukwa mwandikonda ine;" kapena, "Ndikutamandani Ambuye chifukwa Inu ndi Mulungu wamkulu ndi wamphamvu-zonse." Mawu amenewa ndi a chidule akuuza Mulungu monga m'mene Iye alili kwa ine m'moyo mwanga.

Poganizira ife za moyo ndi imfa ya Yesu, tikhoza kudabwa ndi zonse zimene Mulungu, mlengi wa dziko lonse, watichitira ife. Chikondi chake ndi chopambana choposa kuti sitingachizin-dikire. Zochita zake ndi zazikulu ndi zabwino koposera zina zimene tingaziyamikire. Ino ndi nthawi yabwino ya kuima kanthawi ndi kuthokoza Mulungu.

Cholinga cha kupachikidwira kwake kwa Yesu chinali kukhala nsembe ya machimo athu. Iye analangidwa, kuweruzidwa wolakwa chifukwa cha machimo anu amene mwachita ndi amene mudzachita. Tiyenera kumthokoza ndi kumpembedza Iye tsiku lililonse pokhala Iye Mbuye ndi Mpulumutsi.

Tikufuna kupemphera mapemphero apafupi monga ndime. Munthu aliyense apemphere pemphero ganizo kapena lingiriro limene labwera m'maganizo mwake ndipo m'mene akufuna kufotokozera Mulungu. Tiyeni tigwetse nkhope zathu pansi ndi kuganizira za Mulungu, za Yesu, zimene Iye anazichita pa utumiki wake pa dziko lapansi, zimene anazichita pa mtanda, za kuuka kwake, za kubweranso kwake kwachiwiri, ndi zimene ali kuchita tsopano m'mitima yathu. Munthu aliyense akhoza kupemphera nthawi zambiri monga momwe afunira motsogoledwa ndi Mzimu Woyera. Iyi ndi nthawi yogawana poyera zimene zili mkati mwa mtima mwathu. Pitirizani mowirikiza monga momwe zifunikira. Tsono pitani pa pemphero lina pa zosowa ndi kupemphererana wina ndi mnzake.

**Mtsogoleri, kumbutsani anthu onse kuyamba kukhala ndi nthawi yopembedza Mulungu tsiku lililonse mu nthawi yawo yapadera ndi Iye. Tsimikizirani kuti sabata ndi sabata mufunsa aliyense m'mene nthawi yawo yapadera ili kuyendera. Alimbikitseni iwo amene ali ndi mavuto, ndipo lolani anthu kugawana zinthu zimene Mulungu waonetsera kapena zinthu zabwino zimene Mulungu wachitira iwo.*

Kuyamba Moyo Watsopano mwa Yesu

Nkhani Zoona Zochokera mu Buku la Mateyu

Kuuka Kwake Kwa Yesu Kwa Akufa

Phunziro 8, Mateyu 27

"Pakuti ndidziwa malingiriro amene ndilingirira inu, ati Yehova, malingiriro a mtendere, si a choipa, akukupatsani inu adzukulu ndi chiyembekezero." Yeremiya 29:11

KUBWEREZA

1. Mneneri Yesaya analosa kuti Yesu adzatchedwa "Imanuele" limene limasulidwe kutanthauza chiyani?
2. Yesu ananena kuti ndi yani yekha amene akudziwa tsiku limene Iye adzabweranso?
3. Yohane anabatiza anthu ambiri amene anadza kwa iye m'chipululu. Kodi iwo analapa chiyani?
4. Yesu anayankha Satana katatu pogwiritsa ntchito chiyani?
5. Ngati timafuna kumudziwa Mulungu bwino, ndi chofunikira kuti tichite chiyani naye tsiku ndi tsiku?
6. Yesu akuitana omtsatira Iye kukhala asodzi a chiyani?
7. Yesu anawauza ophunzira ake kuti popeza Iye ali pakati pawo, iwo sayenera kuchita chiyani?
8. Yesu anagwidwa nacho chifundo ndi anthu chifukwa cha zinthu zambiri zotani za iwo?
9. Yesu anauza ophunzira ake kukhala ochenjera ngati chiyani? Anawauzanso kuti akhale ofatsa ngati chiyani?
10. Ku bwalo kwake kwa Kayafa, kodi Petro anapereka Yesu bwanji?
11. Kodi Yudasi analipiridwa chiyani popereka Yesu kwa ansembe?
12. Kodi Yesu amachita chiyani ndi machimo athu onse tikawavomereza?
13. Kodi asirikali a Chiroma anachita chiyani ndi Yesu?
14. Akulu a ansembe anadza pansi pa mtanda kumchita chiyani Yesu pokufa Iye?
15. Zinthu zambiri zachilendo zinachitika pamene Yesu anamwalira, ngakhale kuti anthu ena amene anamwalira kale anauka kwa akufa, ndipo anaoneka m'Yerusalemu pa kuchita chiyani?
16. Yosefe wa ku Arimateya anatenga thupi la Yesu naliika kuti?

Tsiku linzake Yesu atapachikidwa, akulu a ansembe ndi Afarisi anakomana pamodzi ndi Pilato. Anamuuza Pilato kuti Yesu analosera kuti Iye adzauka m'manda tsiku lachitatu. Anamfunsa ngati chitetezo china chokwanira chikhoza kuchitika kutsimikiza kuti wina aliyense asabe mtembo wake wa Yesu. Pilato anavomera pempholo. Choncho gulu lina la iwo linapita ku manda kukaika chizindikiro cholimbitsa pa khomo ndi mphanga. Ndiponso anaika asirikali azida kuti azilondera malowo.

Tsopano m'mawa wa tsiku lasabata, kuyamba kwa Sabata, Maria Magadala ndi Maria wina anabwerera ku manda. Koma pamene anafika kunali chivomezi chachikulu choti chimwala chimene chinatsekera khomo la manda chinachotsedwa. Mngelo wa Ambuye amene anatsika kuchokera kumwamba anakhala pansi pamwamba pa chimwala chija. Zovala zake za mngeloyo zinali zoyera ngati matalala ndipo maonekedwe ake anali ngati mphezi. Asirikali amene analondera manda ananjenjemera ndi mantha nakhala ngati anthu akufa.

Mngelo anauza azimayiwo kuti asachite mantha. Ananena, "Musaope inu; pakuti ndikudziwa kuti mukufuna Yesu, amene anapachikidwa. Iye mulibe muno iyayi; pakuti anauka, monga ananena. Idzani muno mudzaone malo m'mene anagonamo Ambuye. Ndipo pitani msanga, muuze ophunzira ake kuti wauka kwa akufa; ndipo onani, akutsogolerani ku Galileya; mudzamuona Iye komweko; onani, ndakuuzani inu."

Azimayiwo anachoka msanga kumanda ndi mantha ndi kukondwera kwakukulu, nathamanga kukauza ophunzira ake. Koma pamene anali pa njira Yesu anakomana nawo nati, "Kondwerani!" Ndipo anadza namgwira Iye pa mapazi, namgwadira. Pomwepo anawauza, "Musaope. Pitani kauzeni abale anga kuti amuke ku Galileya ndipo adzandiona ine komweko."

Asirikali aja amene analondera manda analowa m'mzinda napereka lipoti kwa ansembe akulu zimene zinachitika. Ansembe aja anakhala upo, napatsa asirikaliwo ndalama zambiri nati, "Kazinenani kuti ophunzira ake anadza usiku namuba Uja m'mene ife tinali m'tulo." Anawauzanso kuti, "Ngati ichi chidzamveka kwa Pilato, ife tidzamgwetsa mtima, ndipo tidza-kukhalitsani opanda nkhawa." Tsono asirikali aja analandira ndalamazo, nachita monga anawalangiza. Mbiriyo inabuka mu Yerusalemu kufikira zaka zambiri, ngakhale mpaka lero.

Ophunzira khumi ndi mmodzi otsalawo anapita ku Galileya ku phiri limene Yesu anawauza kuti akawapeza. Pamene anamuona Yesu, onse anampembedza Iye, koma ena anakayika. Tsono Yesu analankhula nawo nthawi yotsiriza nanena, "Pitani kwa anthu a mitundu yonse, mukawasandutse ophunzira anga, ndi kuwabatiza m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera; ndi kuwaphunzitsa kuti asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu. Ndipo ineyo ndili nanu masiku onse, kufikira kutha kwa dziko lino lapansi." Amen.

MAFUNSO

1. Ndi chifukwa chiyani Afarisi anafuna kuika alonda pa manda ake a Yesu?
2. Azimayi awiri amene anabwera kudzaona manda a Yesu anali ayani?
3. Nanga azimayiwo anaona chiyani atafika ku manda?
4. Mngelo anawauza chiyani?
5. Chinachitika chiyani ndi alonda?
6. Mngelo ataonekera, kodi alonda aja anapita kuti?
7. Kodi akulu a ansembe anawalonjeza chiyani alondawo?
8. Kodi azimayi anaona ndani ali pa njira kuthamangira kukauza ophunzira a Yesu?
9. Yesu anapereka uthenga kwa ophunizira ake kuti akomane naye kuti?
10. Pamene Yesu anali pa phiri asananyamulidwe kumwamba, kodi analamulira omtsatira Iye chiyani?
11. Kodi Yesu analonjeza kuti adzakhala ndi yani kufikira malekezero ake a dziko lapansi?

ZOONA ZA UZIMU

1. <u>Uthenga wa Yesu uyenera kugawidwa ndi anthu onse</u>. Mwina Mulungu ali kugwira ntchito mkati mwa mtima mwanu kukupatsani inu mphamvu ndi njala ya kugawa uthenga wake kwa anthu ena. Kuli njira zambiri za kuuza ena za chikondi chake cha Yesu. Njira imodzi yabwino ndi kutsogolera munthu kapena gulu kuphunzira za nthano yake ya Yesu. Mukhoza kuchita zimenezi pa kugwiritsa ntchito maphunziro awa kwa masabata asanu ndi atatu. Kuchokera pa phunziro la chinayi, ife, monga gulu, tili kupempherera anthu ena amene Ambuye atitsogolera m'mitima yathu. Ndikuyembekezera kuti munakhala ndi nthawi ya kuuza anthu pang'ono za m'mene Mulungu wasinthira mtima wanu. Ngati si choncho, pangani sabata ino kukafikira iwo.
   *Musapite kwa munthu ndi kukamuuza iye zovuta zake, kuti Mulungu adzamtumiza iye ku moto woopsya ngati iye salapa.
   *Koma pitani mukamuitanire kukhala ndi maphunziro achidule a Mawu a Mulungu ndi inu kunyumba kwake. Mumuuze kuti inu mwaphunzira m'Mawu a Mulungu ndipo mwaganiza kuti mwina iye adzafunanso kuphunzira ndi inu m'menemo za moyo wa Yesu masabata asanu ndi atatu.
   *Popita ku nyumba kwake, tengani mnzanu ndi inuyo, mwina mwake wina wa pa gulu lanu la maphunzirowa kapena munthu wina amene mukomana naye ku mpingo, kapena mtsogoleri wa gulu lanu ili.
   *Nthawi imene mupita, khalani ndi nthawi kulankhula ndi munthuyo za zinthu zimene zili kumchitikira m'moyo mwake. Komanani ndi abale a pa banja lake; mvetserani zosowa zawo. Mumpempherere iye, ntchito yake, banja lake, ndi kupempha Mulungu kubweretsa mtendere ku nyumba kwake.

*Yambani maphunziro anu ndi nthano ya kubadwa kwake kwa Yesu Khristu. Mloleni iye kufunsa mafunso. Ngati inu simudziwa yankho, chabwino. Mungomuuza kuti inuyo mudzakambirana ndi mtsogoleri wa gulu lanu lophunzira Mawu a Mulungu, ndipo mudzamfunsa iye funso limenelo, chifukwa chakuti inuyo simudziwa yankho lake, ndipo kuti mudzabweretsa yankho lake sabata lina lobwereralo.
*Musakhale pa nyumba yake kokwanira ola limodzi. Kumbukirani kuti iyi ndi phunziro la Mawu a Mulungu la chidule.
*Tsiku lililonse m'sabata limenelo, ndi sabata lililonse pa masabata a patsogolo, pemphererani munthu ameneyo ndi banja lake. Pemphani anthu a gulu lanu kulumikizana nanu m'mapemphero owapempherera iwo.

KUMBUKIRANI: Monga momwe ife tilibe mphamvu yochiritsa wina aliyense kapena kuchotsa ziwanda, tilibenso mphamvu yotembenuza anthu pa chosowa chawo cha Yesu. Iye amene ali ndi mphamvu ndi Mzimu Woyera amene amakhala mwa ife. Iye ali ndi mphamvu yochiritsa nthenda za anthu; Iye ali ndi mphamvu yochotsa ziwanda mu miyoyo ya anthu, Iye ndi yemwe ali ndi mphamvu yodula maunyolo a uchimo ku miyoyo ya anthu ndi kuwabweretsa iwo kwa Yesu. Udindo wathu ndi kugawana nawo ndi kuwapempherera. Mwina mukhoza kukhala pa malo ena amene inuyo mulibe danga lophunzira Mawu a Mulungu kwa masabata asanu ndi atatu ndi munthuyo, koma kwenikweni mukufuna kugawana naye za Yesu Khristu.

Zimene muyenera kuchita:
*Muuzeni iye, monga mungathe pokumbukira, nthano ya Yesu Khristu. Muuzeni za kubadwa kwake, ubatizo wake, moyo wake, zozizwitsa zake, chikondi chake, uthenga wake wa kulapa, kuperekedwa kwake, imfa yake, ndi kuuka kwake.
*Muuzeni kuti monga anthu a mu nthawi ya Yesu, ife tonse tachita zolakwa zambiri pa maso pa Mulungu, ngakhale kuti ife ndife anthu abwino. Izi zitanthauza kuti tonse ndife ochimwa. Mumpatse iye zitsanzo zina za machimo: bodza, kuba, udani, nsanje, chigololo, kusamvera Mulungu, ndi zina.
*Muuzeni kuti monga momwe Mulungu anakhululukira anthu akale, anakhululukira inunso pamene munalapa machimo anu.
*Fotokozerani mwa chidule za moyo wanu musanalandire Yesu m'moyo mwanu, nthawi imene munasankha kutsatira Yesu, ndi moyo umene mulili tsopano (umboni wanu).
*Werengani ndime imodzi yopambana ya m'Mawu a Mulungu: Yohane 3:16.
*Funsani iye ngati akufuna kulapa machimo ake, kukhulupirira Yesu Khristu, ndi kulandira chikhululukiro cha Yesu.
*Fotokozerani kuti kukhulupirira kutanthauza kuti ndi kutembenukira moyo wanu kwa Khristu. Uku ndi kudalira Iye ndi kupereka moyo wanu kwa Iye.
*Ngati atanena, "Inde," muthandizeni iye kupemphera pemphero la chidule kupereka moyo wake kwa Mulungu.
*Ngati atanena, "Ayi," mufunseni iye ngati angavomere inu kumpempherera iye pamenepo. Kenaka pempherani kwa Mulungu kuti akhoza kumuthandiza kuzindikira choonadi chake cha moyo wake.

*Imani ndi kutenga nthawi m'gulu lanu kuyesa kuchitira umboni wanu kwa munthu wina. Gawanani mwa anthu awiri awiri, ndipo mulole wina aliyense kuti apitirize kugawanako.

Pambuyo pa kuchita zimenezi, mwina mudzaganiza, "Ichi nkosatheka. Ine sindingathe kuuza wina za Yesu." Ganizirani choonadi chotsiriza cha maphunzirowa:

2. "<u>Ndipo ineyo ndili nanu masiku onse, kufikira kutha kwa dziko lino lapansi</u>." Mawu a Mulungu amaphunzitsa kuti kuyambira nthawi imene tilandira Yesu, Mzimu Woyera wa Mulungu walowa nthawiyo m'moyo mwathu. Simungathe kuzindikira izi, koma ali kale kugwira ntchito m'moyo mwathu. (Yohane 14:7)
*Iye ndi yemwe amatiphunzitsa ife mu nthawi yathu ya patokha ndi Mulungu tsiku lililonse. (Yohane 14:26)
*Iye amatikumbutsa ife nthawi imene tikhala osamvera Mulungu. Iye ndi yemwe amatithandiza ife kuzindikira pa nthawi yathu yoyamba imene ife tinali ochimwa ndi kusowa Yesu Khristu kukhululukira machimo athu. (Yohane 16:8-11)
*Iye ndi amene amatipatsa ife nzeru, ndi kutitsogolera ife kufikira ungwiro wake wa Mulungu ku moyo wathu. (Yohane 16:13)

*Iye amatitonthoza ife nthawi imene tikumva chisoni. (Machitidwe 9:31)
*Iye amatipatsa ife mphamvu ndi mphatso zina zapadera kuti tikhoza kuchita zinthu zonse zimene amatiuza. Amatipatsa mawu a kuuza ena za Yesu Khristu (1 Akorinto 12).

Tikhoza kuganiza kuti ife sitingakhale otsatira a Yesu amene tiyenera kukhalira. Timaganiza kuti kumvera Mulungu ndi chinthu chovuta. Choonadi ndi chakuti izi ndi zoona. Ife sitingathe kuchita china chilichonse kutsatira Yesu, koma Mulungu akhoza, kupyolera mwa Mzimu Woyera amene amakhala mkati mwa miyoyo yathu.

Ichi ndi chinsinsi cha kuuza ena za Yesu Khristu; ndi chinsinsi chokhala moyo wopanda mantha; ndi chinsinsi chochitira zisankho zoyenera tsiku lililonse. Nthawi imene tilola mlengi wa dziko lonse kulowa mkati mwa miyoyo yathu, Iye amatipatsa ife mphatso ya kukhala Iye ndi ife nthawi zonse. Kukhalapo kwa Mzimu Woyera ndi gwero la mphamvu zathu. Ichi ndi chinthu chopambana chifukwa Mawu a Mulungu amatiphunzitsa ife kuti Mulungu ali ndi dongosolo lodabwitsa ndi cholinga chabwinodi kwa wina aliyense pa moyo wathu. Tiyeni titsirize phunziroli ndi lonjezo lopambana lopezeka pa Yeremiya 29:11-13:

“Pakuti ndidziwa malingiriro amene ndilingirira inu, ati Yehova, malingiriro a mtendere, si a choipa, akukupatsani inu adzukulu ndi chiyembekezero. Pamenepo mudzandiitana Ine, ndipo mudzankha ndi kupemphera kwa Ine, ndipo ndidzakumverani inu. Ndipo mudzandifuna Ine, ndi kundipeza, pamene mundifuna ndi mtima wanu wonse.”

Mulungu akudalitseni inu pamene mupitiriza kumufuna ndi kumudziwa Iye!